# Buku la Mphunzitsi

## Nthawiyabaibulo
## Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi

### Maphunziro C7 - C12

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**

Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**

Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**

A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| MAPHUNZIRO A | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO B | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO C | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

### C7 – KALASI 3
**Phunziro Loyamba – Moyo wa Davide**
**Mutu – Kusankha mfumu**

**Werengani:** *1 Samueli 16: 1-13*
**Vesi Yoloweza:** *1 Samueli 16: 7*

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Sauli analephera monga mfumu ya Israyeli, choncho pankafunika kukhala mfumu yatsopano.
2. Mulungu amakhudza kwambiri ndi chomwe tili 'mu mtima' mwathu kuposa maonekedwe athu, ndipo ndi Mulungu yekha amene amadziwa za 'm'mitima' mwathu.

### C7 – KALASI 4
**Phunziro Loyamba – Moyo wa Davide**
**Mutu – Kusankha mfumu**

**Werengani:** *1 Samueli 16: 1-13*
**Vesi Yoloweza:** *Machitidwe 13: 22*

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Sauli anakanidwa ndi Mulungu kukhala mfumu ya Israyeli chifukwa cha kusamvera kwake Mulungu, choncho panafunika kukhala mfumu ina yatsopano.
2. Mulungu amaweruza potengera chikhulupiriro ndi khalidwe osati maonekedwe akunja. (Maonekedwe saulula chomwe munthu ali kapena kuyenera kwake.)

## MAWU OYAMBA

**Kalasi 3:** Sauli anali mfumu yoyamba ya Israyeli ndipo iye ankasamala kwambiri za maonekedwe osati za kumvera malamulo a Mulungu. Mulungu anamukana kukhala mfumu ya Israyeli komabe analola kuti akhale mfumu nthawi yonse ya moyo wake. Koma iye sanaloledwe kupereka ufumu wake kwa ana ake pamene anamwalira. Mosiyana ndi Sauli, mfumu yotsatira, Mfumu Davide, adzasankhidwa chifukwa cha khalidwe la 'mtima' wake koma osati chifukwa cha maonekedwe ake.

**Kalasi 4:** Mulungu anawuza Sauli kuti akaononge Aamaleki pamodzi ndi katundu wawo – dziko limene linathira nkhondo yachibisaliro a Israyeli ena pamene ankachokera ku Aigupto kupita ku Kanani. Mulungu anadziwa kuti Aisrayeli sakhala pa mtendere ngati Aamaleki alipo. Sauli sanamvere lamulo la Mulungu ndipo zotsatira zake Mulungu anamukana kukhala mfumu ya Israyeli ngakhale anamulola kukhalabe mfumu mpaka imfa yake.

## KUTSIRIZA

**Kalasi 3:**

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Samueli, mneneri, anatumidwa ndi Mulungu kupita ku Betelehemu kuti akadzodze mwana mmodzi wa Jese kuti adzakhale Mfumu ya Israyeli m'tsogolo. Ichi ndi chifukwa chakuti Sauli anali atakanidwa kukhala mfumu. ***(16: 1)***
2. Samueli anayang'ana pakati pa ana asanu ndi awiri a Jese amene analipo pa phwandolo, ndipo anali ndi chitsimikizo kuti mmodzi mwa iwo adzakhala mfumu ya Israyeli m'tsogolo, koma Mulungu anawuza Samueli kuti palibe pakati pawo amene Iye wamusankha. ***(16: 10)***
3. Samueli anafunsa ngati analiponso ana ena aamuna ndipo anabwera ndi kamnyamata kotchedwa Davide kuchokera koweta nkhosa. Mulungu anawuza Samueli kuti adzodze, pakuti Mulungu ankadziwa 'mtima' wake kuti unali wabwino. ***(16: 11-12)***
4. Anathira mafuta pa mutu pa Davide ndipo izi zinasonyeza kuti Davide wapatulidwa kuti agwire ntchito ya Mulungu. ***(16: 13)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kusankha mfumu.

**Kalasi 4:**

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Mulungu anatuma Samueli kupita kwa Betelehemu kuti akadzodze mwana mmodzi wa Jese kuti adzakhale Mfumu ya Israyeli m'tsogolo. Ichi ndi chifukwa chakuti Sauli anali atakanidwa kukhala mfumu. ***(16: 1)***
2. Samueli anayitana Jese ndi ana ake aamuna ku phwando la nsembe kuti adzaone ana asanu ndi awiri a Jese kuti apeze amene adzakhale mfumu ya Israyeli, koma Mulungu anamuwuza kuti: 'Yehova sanasankhe awa.' ***(16: 10)***
3. Samueli anafunsa Jese ngati anali ndi ana ena ndipo anawuzidwa za Davide, mwana wamng'ono, amene ankaweta nkhosa. Samueli anayitanitsa Davide kuti abwere pamaso pake ndipo Yehova anamuwuza kuti Davide ndiye adzakhale mfumu m'tsogolo. ***(16: 11-12)***
4. Samueli anadzodza mafuta Davide ndipo izi zinasonyeza kuti Davide tsopano wapatulidwa ndi Mulungu kuti adzagwire ntchito yake m'tsogolo. ***(16: 13)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kusankha mfumu.

## KUKUMBUTSANA

**Kalasi 3:** Kambiranani nkhaniyi ndi ophunzira ndipo tsindikani kufunika kwa kusaweruza anthu poona zinthu za kunja monga maonekedwe, mavalidwe ndi chuma chawo. Langizani ophunzira kuti atolonkhani ndiye amalimbikitsa kuweruza kolakwikaku pogwiritsa ntchito amene akuoneka kuti zinthu zikuwayendera akufuna kulengeza zinthu zawo pa kanema, mu nyuzi ndi m'magazini awo. Mosiyana ndi zimenezi, Mulungu amaweruza potengera chikhulupiriro ndi khalidwe la munthu, zomwe Iye yekha ndiye amatha kuziona. Mulungu ali ndi chikonzero ndi miyoyo yathu ndipo angathe kugwira ntchito mwa ife ngati tamudalira Iye ndi kumulola kukhala Ambuye wa miyoyo yathu.

**Kalasi 4:**
1. Funsani ana abwereze phunziro ili popereka mayankho a mafunso awa m'mawu awo:
2. Kodi Samueli anatumidwa ndi Mulungu kuti akachite chiyani pa ***vesi 1-3***?
3. N'chifukwa chiyani Samueli anaganiza molakwika za Eliyabu pa ***vesi 6 ndi 7***?
4. Kodi Mulungu anasankha ndani kuti akhale mfumu ya Israyeli, nanga Samueli anachita chiyani pofuna kutsimikizira kuti iye ndiye anali woyenera pa ***vesi 11-13***?

## KHALANI MOYO UMENEWU

**Kalasi 3:**

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Zomwe tikuyenera kuchita kuti tikonze 'khalidwe la mu mtima' mwathu.
2. Kutsogolo kunali zaka zambiri kuti Davide adzavale mkanjo wa Sauli, koma Mulungu ankamukonza iye kuti adzamutumikira m'tsogolo. Ngati ife tikudalira Ambuye Yesu, nthawi zonse tikuyenera kumapemphera kuti Mulungu azitipatsa mphamvu ndi kulimba mtima kuti Iye akwaniritse chikonzero chake pa miyoyo yathu.

**Kalasi 4:**

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Davide anali wosiyana ndi Sauli komanso ndi abale ake onse. Iye ankamvera Mulungu ndipo Mulungu anamudalitsa. Kodi ili nthawi pa moyo wanu, kapena pa zochitika zina pamene mumaona kuti kumvera Mulungu ndi Mawu ake kumakhala kovuta?
2. Mulungu amakonda chomwe ife tili m'kati mwathu, m'mitima mwathu, kuposa maonekedwe athu akunja. Tisamaweruze anthu potengera maonekedwe awo akunja koma potengera chikondi chomwe ali nacho pa Yesu. Funsani kuti akupatseni zitsanzo.

| | C7 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Davide<br>Mutu – Kumenyana ndi Goliati | C7 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Davide<br>Mutu – Kugonjetsa munthu wamphamvu! |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Samueli 17: 12-52***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 17: 47***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Davide anadzipereka kupita kukamenyana ndi Goliati.<br>2. Monga Davide anali wokonzeka ku uzimu kukumana ndi Goliati, nafenso titha kukhala okonzeka kulimbana ndi mdierekezi powerenga Mawu a Mulungu ndi kuchita mawuwo mseri komanso pakati anthu ena. | **Werengani:** ***1 Samueli 16: 14-19; 17: 12-52***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 17: 47***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Davide ankakhulupirira Ambuye kuti adzamupambanitsa pamene ankapita kukamenyana ndi Goliati.<br>2. Ngati ife timadziwa Ambuye Yesu ngati Mpulumutsi wathu, ifenso titha kumugonjetsa Satana m'miyoyo yathu chifukwa Ambuye Yesu anamugonjetsa pamene anafa pa mtanda. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira kuti Davide anali atadzodzedwa kuti adzakhale Mfumu ya Israyeli. Kupha Goliati kunaonetsa poyera chifukwa chimene Mulungu anamusankhira. Pamene chiphona cha Afilisti chinkaopseza ankhondo a Israyeli, Sauli ndi asilikali ake ankachita mantha. Koma Davide anadalira Mulungu ndipo anapambana, kuonetsa kuti mphamvu yeniyeni sibwera chifukwa cha msinkhu kapena mphamvu za munthu koma kudalira Mulungu. | Pamene ana a Israyeli anafika koyamba ku Dziko la Malonjezano, ambiri a iwo anachita mantha kuti alowemo chifukwa cha ziphona zimene zinkakhala kumeneko. ***(Numeri 13: 32-33)***. Pa ***Deuteronomo 3: 11***, Baibulo likutiwuza za Mfumu Basana amene ankagona pa bedi lotalika mamita 4! Tsopano Goliati anali wotalika mamita 3, ndipo ankanyoza asilikali a Israyeli mbali ina ya chigwa cha Ela. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Davide anabweretsa zakudya kwa abale ake atatu amene anali ku nkhondoko ndipo anaona nkhope za mantha za asilikali a Israyeli pamene chiphona Goliati (wamtali mamita atatu) ankabwera kudzawanyoza. ***(17: 20-24)***<br>2. Werengani maonekedwe a zida zake ndi zodzitetezera za Goliati. ***(17: 4-7)***<br>3. Davide anafunsa kuti ndi mphotho yanji yomwe idzaperekedwa kwa munthu amene adzapha Goliati, koma m'bale wake Eliyabu anamudzudzula kwambiri chifukwa chobwera ku nkhondo. ***(17: 26-29)***<br>4. Davide anati adzapita kukamenyana ndi Goliati. Sauli anakayikira mphamvu za Davide kuti angaphe Goliati. Koma iye anadziwa kuti mphamvu ya Mulungu inkagwira ntchito mwa Davide pamene anamuwuza zomwe zinachitika pamene anateteza nkhosa za abambo wake kwa mkango ndi chimbalangondo. Davide anadziwa kuti akhoza kudalira Mulungu kuti adzamupulumutsa. ***(17: 34-37)***<br>5. Davide anayenda kupita kumene kunali Goliati, ndipo anamugenda mwala wake oyamba ndi legeni yake. Iye anagenda pa chipumi cha Goliati, ndipo anagwa pansi. Davide anamupha pogwiritsa ntchito lupanga la chiphonacho ndipo Afilisiti onse anathawa akuthamangitsidwa ndi Aisrayeli! ***(17: 40-52)***<br>6. Mulungu anaonetsa mphamvu zake popereka kwa Davide chipambano.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kumenyana ndi Goliati. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ankhondo a Afilisti ndi ankhondo a Israyeli anasonkhana moyang'anana m'mbali mwa chigwa cha Ela kuti amenyane. Goliati anali ndi zida za nkhondo zamphamvu ndipo kwa masiku makumi anayi ankawuza ankhondo a Israyeli kuti atumize munthu amene adzamenyana naye. ***(17: 1-10)*** Werengani maonekedwe a zida ndi zodzitetezera za Goliati. ***(17: 4-7)***<br>2. Davide anaona zomwe zinkachitika komanso mantha a Aisrayeli pamene anabweretsa zakudya za abale ake amene anali ku nkhondo. Davide ankadziwa kuti Mulungu anali naye m'mbuyomo ndipo anadzipereka kukamenyana ndi Goliati, akudziwa kuti Mulungu anadzaonetsa kuti apambane. ***(17: 26-29)***<br>3. Sauli anakayika koma ataona kulimba mtima kwa Davide, anamupatsa zida zake, zomwe Davide anazikana akuti zinkamulemera. ***(17: 31-39)***<br>4. Ndi miyala yabwino isanu, legeni ndi ndodo, iye anapita kukakumana ndi Goliati amene anakwiya kwambiri kuti munthu wosadziwika bwino monga Davide anatumizidwa kuti adzamenyane naye. ***(17: 40-44)***<br>5. Davide anali katswiri wodziwa kugenda ndipo anagwetsa Goliati ndi mwala wake oyamba, umene anamenya pa chipumi cha Goliati. Goliati anagwa chafufumimba ndipo Davide anagwiritsa ntchito lupanga lake lomwe kumupha, zomwe zinachititsa Afilisiti kuthawa ndipo Aisrayeli kumawathamangitsa. ***(17: 40-52)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kugonjetsa munthu wamphamvu! |
| **KUKUMBUTSANA** | Werengani ***Aefeso 6: 10-17*** ndi kufotokoza kwa ophunzira kuti 'zida za uzimu' ndi zomwe Davide anavala zinali ziti pamene anapita kukamenyana ndi Goliati. Fotokozani kuti monga Akhristu, ngati tikudalira Ambuye tikuyenera kuvala 'zida za uzimu' kuti timenyane nkhondo zimene timakumana nazo tsiku ndi tsiku pa miyoyo yathu ya Chikhristu. | 1. Werengani ***Salimo 108: 12-13*** ndipo funsani ophunzira kuti afotokoze kuti mavesi amenewa akunena zoona zotani za Davide pamene anapha Goliati.<br>2. Werengani ***1 Akorinto 15: 57*** ndi kufunsa kuti chipambano cha Davide pa Goliati chikufanana motani ndi chipambano cha Ambuye Yesu pa Satana.<br>3. Werengani ***Aefeso 6: 10-18*** ndi kufunsa ophunzira kuti akambirane mitundu ya zida za Mkhristu kuti agonjetsa Satana. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ambuye Yesu anapambana nkhondo yayikulu kwambiri pamene anafera ochimwa ndi kugonjetsa Satana. Chifukwa anapambana, Iye angathe kutipatsa mphamvu zogonjetsera mayesero a Satana. Onani ***Ahebri 2: 14***.<br>2. Kutsutsidwa sikunalepheretse Davide kuchita kanthu chifukwa ankadziwa kuti iye anali ndi Mulungu ndi kuti Mulungu anali mbali yake. Ife tikuyenera kupitirira kuchita zimene tikudziwa kuti ndi zolondola ndi zokondweretsa Mulungu – amene maganizo ake ndiye wofunika kwambiri. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Davide ankadziwa kuti Mulungu amumenyera nkhondo akakumana ndi Goliati. Tikakumana ndi mayesero ochokera kwa Satana, Ambuye adzatimenyera nkhondo tikamudalira Iye.<br>2. Kudalira Mulungu kwa Davide kunali kwa mphamvu chifukwa Mulungu anamuteteza m'mbuyomo. Ife tikakumana ndi mavuto, tizikumbukira momwe Mulungu anatithandizira kuti titha kukumana ndi zovuta zam'tsogolo. |

| | **C7 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Moyo wa Davide**<br>**Mutu – Kukhala ndi Sauli** | **C7 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Moyo wa Davide**<br>**Mutu – Kupirira m'mavuto!** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Samueli 18: 1-17; 19: 1-18***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 18: 14***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngakhale Davide anali mnyamata amene anasankhidwa ndi Mulungu kukhala mfumu, iye anakumana ndi mavuto ambiri pa moyo wake asanakhale mfumu ya Israyeli, koma Davide anadalira Mulungu wake kuti adzamuthandiza kuthana ndi mavutowo.<br>2. Monga Mulungu anateteza Davide pa ziopsezo zake zonse, momwemonso Mulungu amathandiza amene amamudalira mu nthawi zawo zovuta kwambiri ndi zoopsa. | **Werengani:** ***1 Samueli 18: 1-23; 19: 1-18***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 13: 5-6***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngakhale Davide anali mnyamata amene anasankhidwa ndi Mulungu kukhala mfumu, iye anakumana ndi mavuto ambiri pa moyo wake asanakhale mfumu ya Israyeli, koma Davide anadalira Mulungu wake kuti adzamuthandiza kuthana ndi mavutowo.<br>2. Akhristu amakumana ndi mayesero ndi zovuta; chikhulupiriro chawo mwa Ambuye Yesu chidzawathandiza kukhala ogonjetsa ndi kuwapatsa mphamvu kuti akhale moyo chifukwa cha Iye. |
| **MAWU OYAMBA** | Bwerezani nkhani ya Davide mpaka pamene yafika. Davide anabwera kudzakhala ndi Mfumu Sauli, ndipo ubale wabwino unayamba pakati pa mwana wa Sauli, Jonatani, ndi Davide. Jonatani ndi amene ankayenera kulowa ufumu koma iye anali wokonzeka kusiya ndi cholinga choti Davide akhale mfumu. Davide ankapambana pa nkhondo zake ndi Afilisti ndipo izi zinachititsa kuti atchuke pakati pa anthu, koma Sauli anachita naye nsanje kwambiri ndipo ankafuna njira zoti amuphe. | Bwerezani nkhani mpaka pamene yafika. Ngakhale Sauli ankachitira nsanje Davide, Jonatani, mwana wa Sauli, anali pa ubwenzi wabwino ndi Davide, ngakhale Jonatani ankadziwa kuti m'tsogolo Davide adzakhala mfumu ya Israyeli. Ngakhale Sauli anayesetsa kufuna kupha Davide nthawi zambiri, Mulungu anagwiritsa ntchito Jonatani, kulangiza ndi kuteteza Davide potsutsa zolinga zoyipa za Sauli. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Davide anabwera kudzakhala ndi Sauli ndipo Jonatani ndi Davide anakhala abwenzi amphamvu. Sauli anamupatsa Davide udindo waukulu koma anayamba kuchita nsanje ndi Davide chifukwa amayi ankayimba kuti, 'Sauli anapha zikwi zake, koma Davide wapha miyandamiyanda.' ***(1 Samueli 18: 1-7)***<br>2. Nthawi ina Sauli anaponya mkondo kwa Davide ndiponso anayesa njira zambiri zoti Davide akaphedwe ku nkhondo. ***(18: 10-27)***<br>3. Jonatani analangiza Davide kuti akabisale komanso anakumbutsa abambo ake Sauli za kukhulupirika kwa Davide ndi chipambano chake pa adani a Israyeli. ***(19: 1-7)***<br>4. Sauli anasiya kudana naye kwa kanthawi kochepa kenaka anakonzanso chiwembu chofuna kupha Davide, koma Mulungu analepheretsa zolinga zake, ndipo Davide anathawa kupita kwa Samueli ku Rama, kuti akapeze thandizo ndi chitetezo. ***(19: 9-18)***<br>5. Mulungu analola Davide kudutsa nthawi zovuta ndi cholinga cholimbitsa khalidwe lake ndi chikhulupiriro chake.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhala ndi Sauli. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Davide anabwera kudzakhala ndi Sauli ndipo Jonatani ndi Davide anakhala abwenzi amphamvu. Sauli anamupatsa Davide udindo waukulu koma anayamba kuchita nsanje ndi Davide chifukwa amayi ankayimba kuti, 'Sauli anapha zikwi zake, koma Davide wapha miyandamiyanda.' ***(1 Samueli 18: 1-7)***<br>2. Nthawi ina Sauli anaponya mkondo kwa Davide ndiponso anayesa njira zambiri zoti Davide akaphedwe ku nkhondo. ***(18: 10-27)***<br>3. Davide ankakhala mwa nzeru ***(18: 5, 15)*** ndipo zotsatira zake Mulungu ankamuteteza.<br>4. Saulo anapereka mwana wake wamng'ono Mikala kuti akhale mkazi wa Davide chifukwa anapha Goliati, koma chidani cha Sauli chinakula pa Davide. ***(18: 20-28)***<br>5. Nkhondo yayambikanso ndi Afilisti. Ngakhale Jonatani analangiza Sauli kuti asaphe Davide, mkwiyo wake unakula kwambiri, ndipo anayesa kachitatu kuti amuphe, koma Davide anathawa kupita ku Rama kukaonana ndi Samueli. ***(19: 1-18)***<br>6. Mulungu analola Davide kudutsa nthawi zovuta ndi cholinga cholimbitsa khalidwe lake ndi chikhulupiriro chake.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjera A – Kupirira m'mavuto! |
| **KUKUMBUTSANA** | Pa ***Salimo 59***, Davide akufotokoza khalidwe la adani ake, makamaka za anthu amene anatumizidwa ndi Sauli kuti adzamuphe. Afotokozereni ophunzira za kudalira Mulungu kwa Davide ndi mmene iye akutamandira ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha 'chitetezo' chake mu nthawi yoopsa imeneyi pa ***vesi 9, 16 ndi 17***. | 1. Werengani ***Salimo 139: 7-12*** ndi kukambirana kukhudzana kwa zomuchitikira Davide pa mavesi amenewa monga tafotokozera m'phunziro lino.<br>2. Werengani ***Salimo 140: 1-8*** ndi kukambirana kuti ndi ndani (Sauli) amene anali m'maganizo mwa Davide pamene ankalemba salimo limeneli. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Jonatani anali wokhulupirika kwa Davide ndipo anali wokonzeka kuvutika chifukwa cha iye. Kodi tingaphunzire chiyani pa ubale wawo pofuna kuti timvetse za ubwenzi?<br>2. Kupitiriza kupambana kwa Davide ku nkhondo zinali zodziwika kwa ena kuti iye anali ndi Mulungu. Ngati ndinu Mkhristu, kodi abwenzi anu amaonetsa kuti mumakonda Ambuye ndi kukhala moyo wokondweretsa Iye tsiku ndi tsiku? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Davide ndi Jonatani anakhala abwenzi enieni. Maziko a ubwenzi wawo anali kudzipereka kwawo kwa Mulungu ndi kukhala mbali imodzi pamene ubwenzi wawo ukuyesedwa. Kodi inu maziko a ubwenzi wanu ndi chiyani?<br>2. Werengani ***Aroma 12: 17-21*** ndi kukambirana makhalidwe amene anali mwa iwo ndiponso amene akuyenera kukhala mwa Mkhristu, monga kuona mtima, kukhala mwamtendere, kukoma mtima, kukhululuka ndi kuonetsa chikondi. |

## C7 – KALASI 3
**Phunziro Lachinayi – Moyo wa Davide**
**Mutu – Pa ubwenzi ndi Jonatani**

**Werengani:** ***1 Samueli 20: 1-42***
**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 20: 17***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Davide akupitirira kukumana ndi mavuto kuchokera kwa Sauli koma Jonatani ndi wokhulupirika kwa iye.
2. Kukhulupirika ndi chinthu chimodzi chofunika kwambiri pa moyo wathu, ndipo tikuyenera kumasunga malonjezo athu ndi kukhala abwenzi enieni.

### MAWU OYAMBA
Bwerezani nkhaniyi mpaka pamene yafika. Davide anabwera kuchokera ku Rama ndipo anafika kwa Jonatani kuti adziwe chifukwa chimene abambo ake ankafuna kumuphera. Anagwirizana zoti achite kuti adziwe ngati Davide anali pa chiopsezo kapena ayi. M'malo mobwera ku phwando la pa mwezi, Davide sabwera. Ngati Sauli adzafunsa za kusapezeka kwa Davide, Jonatani adzati iye ali ku Betelehemu ku mwambo wansembe ya pa chaka. Ngati Sauli adzakondwera ndi chifukwa chimenechi, Davide sali pa chiopsezo. Koma akadzakwiya ponena kuti Davide wapulumuka m'manja mwake, moyo wa Davide udzakhala kuti uli pa chiopsezo chachikulu.

### KUTSIRIZA
**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Davide anafotokozera Jonatani kuti anaopa chifukwa moyo wake unali pa chiopsezo chochokera kwa m'manja mwa Sauli. ***(20: 1-3)***
2. Jonatani analonjeza Davide kuti adzamuwuza zomwe Sauli adzachite akadzazindikira kuti Davide pa phwando palibe, pogwiritsa ntchito zizindikiro zomwe anagwirizana. ***(20: 5-8)***
3. Jonatani akadzapeza momwe zinthu zidzakhalire, iye adzapita pa malo amene agwirizana ndi kuponya mivi itatu. Malangizo amene adzawuze mnyamata wake, amene adzapite kukatola miviyo, pafupi ndi pamene padzabisale Davide, adzaonetsa ngati Davide akuyenera kubwera kapena kuthawa. ***(20: 18-23)***
4. Sauli anakakamiza Jonatani kuti afotokoze kumene kunali Davide ndipo anapsa mtima kwambiri mpaka anaponya mkondo kuti alase mwana wake! ***(20: 28-33)***
5. Chizindikiro chija chaperekedwa kwa Davide ndipo waona kuti iye akuopa zoona. Anthu awiriwa anakumbatirana ndipo kenaka anasiya aliyense kulowa kwina – Davide anapita kukabisala ndipo Jonatani anapita ku nyumba yaufumu. ***(20: 41-42)***
6. Kumbutsani ophunzira za ***Miyambo 18: 24*** ndi kukambirana kufunika kwa ubwenzi wa Davide ndi Jonatani.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Pa ubwenzi ndi Jonatani.

### KUKUMBUTSANA
Bwerezani ndi kufotokoza mwachidule phunziro lino pofuna ophunzira kuti afotokoza m'mawu awo izi mothandizidwa ndi mavesi amene tapereka:
(i) Kodi nkhani ya Davide inali iti? ***(vesi 1-3)***
(ii) Kodi yankho la Jonatani linali lotani? ***(vesi 4)***
(iii) Kodi Jonatani ndi Davide anagwirizana zotani? ***(vesi 5-23)***
(iv) Kodi Davide analandira uthenga wotani? ***(vesi 24-40)***
(v) Kodi Jonatani ndi Davide anasiyana motani? ***(vesi 41-42)***

### KHALANI MOYO UMENEWU
**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Kambiranani ngati ophunzira ali 'okhulupirika' kwa makolo, m'banja ndi kwa abwenzi. Ngati ndi choncho, kodi kukhulupirika kumeneko ndi 'kumaoneka motani'?
2. Akhristu amene amakonda Ambuye Yesu ali ndi njira zambiri zoonetsera kukhulupirika kwawo kwa Iye. Tchulani njira zina.

## C7 – KALASI 4
**Phunziro Lachinayi – Moyo wa Davide**
**Mutu – Kusamalira ena**

**Werengani:** ***1 Samueli 20: 12-17, 42, 2 Samueli 9: 1-13***
**Vesi Yoloweza:** ***2 Samueli 9: 1***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Davide anali ndi mtima wofuna kusunga malonjezo ake pamene anaonetsa kukoma mtima ku banja la Jonatani.
2. Monga Davide anachitira chifundo Mefiboseti, mwana wa Jonatani, Ambuye Yesu anachitiranso ife chifundo pamene anafera machimo athu pa mtanda.

### MAWU OYAMBA
Bwerezani nkhaniyi mpaka pamene yafika. Davide anabwera kwa Jonatani kuti adziwe chifukwa chimene Sauli akufuna kumuphera, koma Jonatani sankadziwa zoti abambo ake ankafuna kupha Davide. Sauli sanafotokozere Jonatani chikonzero chake chifukwa iye ndi Davide anali abwenzi. Anagwirizana zoti achite kuti adziwe ngati Davide anali pa chiopsezo kapena ayi. M'malo mobwera ku phwando la pa mwezi, Davide sabwera. Ngati Sauli sadzatsutsa zimenezi ndiye kuti Davide sali pa chiopsezo. Koma akadzapsa mtima, ndiye kuti Davide ali pa chiopsezo.

### KUTSIRIZA
**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Jonatani anachenjeza Davide pogwiritsa ntchito chizindikiro kuti moyo wake unali pa chiopsezo. Davide asanapite kukabisala, anthu onse awiri analira atakumbatirana pozindikira kuti sadzakhalanso pa ubale wotere. ***(20: 35-42)***
2. Davide anadziwa kuti sadzaonananso ndi Jonatani, choncho analonjeza kuyang'anira banja la Jonatani iye akadzakhala mfumu. ***(20: 42)***
3. Davide atakhala mfumu, anakumbukira lonjezo limene anachita kwa Jonatani la kuti adzachitira chifundo Jonatani ndi banja lake. ***(2 Samueli 9: 1)***
4. Ziba, wantchito wa Mfumu Sauli, anafotokoza kuti Jonatani anali ndi mwana wamwamuna wolumala wotchedwa Mefiboseti, amene sankayenda kuyambira ali ndi zaka zisanu chifukwa anagwa ndipo ankakhala ku Lodebara. ***(2 Samueli 9: 2-4)***
5. Davide anamuyitana kuti abwere ku Yerusalemu ndipo analamula kuti chuma chonse cha banja lake amubwezere ndi kuti iye azidya tsiku lililonse pa tebulo la mfumu. Ziba ndi ana ake akhale antchito a Mefiboseti, motero anakwaniritsa lonjezo limene anachita kwa Jonatani zaka za m'mbuyomo. ***(2 Samueli 9: 5-11)***
6. Kumbutsani ophunzira za ***Miyambo 18: 24*** ndi kukambirana kufunika kwa ubwenzi wa Davide ndi Jonatani.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kusamalira ena.

### KUKUMBUTSANA
Werengani ***2 Samueli 4: 4*** ndi kukambirana ndi ophunzira zomwe zinachitika kuti Mefiboseti akhale wolumala. Werengani ***Aefeso 2: 1-10*** ndi kukambirana ndi ophunzira kuti monga Mefiboseti anadalitsidwa chifukwa cha chikondi ndi kukoma mtima kwa Davide, moteronso Akhristu timalandira madalitso oposa chifukwa cha chikondi ndi kukoma mtima kwa Ambuye Yesu.

### KHALANI MOYO UMENEWU
**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Chokhumba cha Jonatani, Davide atachoka, ndi chakuti Mulungu adzawayang'anira onse pamodzi ndi mabanja awo. Akhristu akuyenera kuchita chilichonse chimene angathe kuthandiza abale awo ndi abwenzi awo. Kodi mungapereke zitsanzo?
2. Pamene tikuona za moyo wa Davide, tikuona kuti mtima wake unali wabwino ndiponso chikhulupiriro chake mwa Mulungu chinali cholimba. Iye ankadalira Mulungu mu nyengo iliyonse, yabwino kapena yoyipa, ndi kuonetsa chikondi cha Mulungu kwa ena monga mmene akanathera. Kodi ife tikuphunzira chiyani kuchokera pa nkhani imeneyi?

| | C8 – KALASI 3<br>Phunziro Loyamba – Yoswa<br>Mutu – Kutsogolera anthu | C8 – KALASI 4<br>Phunziro Loyamba – Yoswa<br>Mutu – Mtsogoleri watsopano |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yoswa 1: 1-11***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yoswa 1: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mose wamwalira ndipo Yoswa walowa m'malo mwake kukhala mtsogoleri wa Israyeli. Udindo wake unali alowetsa Israyeli m'Dziko la Malonjezano la Kanani.<br>2. Monga Yoswa, Akhristu akuyenera kukhala ndi chikhulupiriro kuti ayambe ndi kuyenda ulendo wa moyo wa Chikhristu. | **Werengani:** ***Yoswa 1: 1-11, 16-18***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yoswa 1: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mose wamwalira ndipo Yoswa walowa m'malo mwake kukhala mtsogoleri wa Israyeli. Udindo wake unali alowetsa Israyeli m'Dziko la Malonjezano la Kanani.<br>2. Ife timakula monga Akhristu pamene tikumvera Mawu a Mulungu, Baibulo, ndi kukhulupirira malonjezo ake, makamaka m'masiku ovuta a miyoyo yathu. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani za Yoswa. Aisrayeli anali atamanga misasa mu chigwa cha Moabu, kummawa kwa Mtsinje wa Yordano. Monga mkulu wa ankhondo, Yoswa ankayenera kutsogolera Aisrayeli kuwoloka Mtsinje wa Yordano kuti alowe Dziko la Malonjezano. Ngakhale Yoswa anali ndi luso la nkhondo, chinali chikhulupiriro chake mwa Mulungu chimene chinamuthandiza pamene analowa m'malo mwa Mose monga mtsogoleri wa dziko la Israyeli. Mose ndi amene anamuphunzitsa, ndipo, ali ndi zaka 90, Mulungu ndiye amene anamupatsa udindo wokhala mtsogoleri wa Israyeli. | Fotokozani za Yoswa. Mose atamwalira, Mulungu anawuza Yoswa kuti atsogolere Aisrayeli kulowa m'Dziko la Malonjezano (lotchedwanso Kanani) ndi kuligonjetsa. Poyamba Mulungu analonjeza Abrahamu kuti adzamupatsa dziko la Kanani ndi zidzukulu zake, ndipo analonjezanso kuwathandiza kuthamangitsa anthu oyipa Akanani. Aisrayeli anapita kukaononga kwathunthu maguwa a Akanani ndi cholinga chakuti pasakhale chilichonse chowasokoneza popembedza Mulungu mmodzi woona yekha. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mose atamwalira, Mulungu anayankhula ndi Yoswa kumuwuza kuti atsogolere Aisrayeli, anthu oposa mamiliyoni awiri, kulowa m'dziko lachilendo limene anawalonjeza. Kumbutsani ophunzira kuti anthuwa anakhala akuyendayenda m'chipululu zaka makumi anayi atachoka ku Aigupto. ***(1: 1-3)***<br>2. Katatu ***(vesi 6, 7 ndi 9)*** Mulungu akuwuza Yoswa kuti akhale wamphamvu ndi wolimba mtima chifukwa ntchito imene ili patsogolo pake si yophweka. Mulungu analonjezanso kuti monga anali ndi Mose Iye adzakhalanso ndi Yoswa.<br>3. Yoswa anawuzidwanso kuti ngati akufuna kukhala wopambana, iye akuyenera kumvera malamulo a Mulungu komanso kuwerenga ndi kuphunzira Mawu a Mulungu nthawi zonse. ***(1: 7-8)***<br>4. Yoswa anamvera malangizo a Mulungu ndipo analamula anthu kuti akonzekere chifukwa m'masiku atatu adzanyamuka. ***(1: 10-11)***<br>5. Kambiranani momwe Yoswa anadziwira kuti limene ankamva linali liwu la Mulungu ndi kuchita zinthu momvera chifuniro cha Mulungu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A - Kutsogolera anthu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yoswa anayitanidwa ndi Mulungu kuti akhale mtsogoleri watsopano wa Israyeli. Iye anali mtumiki wa Mose kwa zaka makumi anayi ndipo anali wokonzeka kugwira ntchito yotsogolera anthu mamiliyoni awiri kupita ku dziko lachilendo ndi kuligonjetsa. Kumbutsani ophunzira kuti anthuwa anakhala akuyendayenda m'chipululu zaka makumi anayi atachoka ku Aigupto. ***(1: 1-3)***<br>2. Mulungu sanangolonjeza kokha Yoswa kuti Iye adzawapatsa Aisrayeli dziko la Akanani ***(vesi 3 ndi 4)***, komanso Iye analonjeza kuti adzakhala nawo ndi cholinga chowapatsa mphamvu ndi kuwalimbitsa mtima. ***(vesi 5 ndi 6)***.<br>3. Mulungu akufotokoza kwa Yoswa ***(vesi 7-9)*** kuti chinsinsi cha chipambano chenicheni ndi kupezeka kwa Mawu a Mulungu m'moyo wa Mkhristu. Mukuyenera kuwerenga ndi kumalingalira, kuloweza ndi kumvera ndiponso kuchita.<br>4. Yoswa anamvera malamulo a Mulungu ndipo anthu, anayamba kuzindikira ulamuliro wa Yoswa monga mtsogoleri wawo ndipo anayamba kumvera malangizo ake. ***(vesi 16-18)***.<br>5. Kambiranani kuti Mulungu sanakonzekeretsa Yoswa kokha kuti agwire ntchito yayikulu imene inali patsogolo pake komanso anakonzekeretsa anthu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Mtsogoleri watsopano. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro ili pokambirana ndi ophunzira zifukwa zitatu zabwino kuti Yoswa akhale wamphamvu:<br>(i) Mulungu analonjeza Yoswa chipambano – ***vesi 5 ndi 6***.<br>(ii) Mawu a Mulungu akhale chomutsogolera chake – ***vesi 7 ndi 8***.<br>(iii) Kupezeka kwa Mulungu ndiye mphamvu yomuthandiza – ***vesi 9***. | Kambiranani ndi ophunzira kufanana kwa pakati pa malangizo a Mulungu kwa Yoswa pa ***vesi 8 ndi 9*** ndi za kufunika kwa 'buku la Chilamulo' m'moyo wake ndi malangizo a Mulungu ku ife mu zowerenga zoonjezera pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku:<br>1) Kodi ***Salimo 1*** akunena chiyani za kufunika kwa Mawu a Mulungu pa moyo wathu?<br>2) Kodi tikuyenera 'kuyenda' motani tsiku ndi tsiku molingana ndi ***Miyambo 3: 5-6***?<br>3) Molingana ndi ***Yakobo 1: 22-25***, kumvera kwathu Mawu a Mulungu kumaonekera pa zinthu zimene timachita. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Chipambano chenicheni cha moyo wa Mkhristu chimabwera pamene adzipereka kuwerenga ndi kumvera Mawu a Mulungu. Funsani ophunzira kuti ngati ali Akhristu, kodi kuwerenga ndi kumvera Mawu a Mulungu pa moyo wawo ndi zofunika motani? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Funsani ophunzira ngati anamvera Mawu a Mulungu ndi kukhulupirira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wawo.<br>2. Ngati ndi choncho, kodi iwo amawerenga ndi kukhulupirira malonjezo a Mulungu amene anawapatsa kuti awapatse mphamvu ndi kuwalimbikitsa monga Akhristu?<br>3. Kodi iwo amatsatira zomwe aphunzira pa moyo wawo wa tsiku ndi tsiku? |

| | **C8 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachiwiri – Yoswa**<br>**Mutu – Kuzonda dziko** | **C8 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachiwiri – Yoswa**<br>**Mutu – Kutumiza azondi** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yoswa 2: 1-24***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11: 31***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yoswa anatumiza azondi ku Yeriko amene Rahabi anawabisa kuti mfumu isawapeze.<br>2. Monga Rahabi anapulumuka ku imfa pamene anakhulupirira Mulungu, nafenso timapulumutsidwa pamene takhulupirira Ambuye Yesu. | **Werengani:** ***Yoswa 2: 1-24***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11: 31***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yoswa anatumiza azondi ku Yeriko amene Rahabi anawabisa kuti mfumu isawapeze.<br>2. Monga Rahabi anapulumuka ku imfa pamene anakhulupirira Mulungu, nafenso timapulumutsidwa pamene takhulupirira Ambuye Yesu. |
| **MAWU OYAMBA** | Tsopano Israyeli yafika pa Yordano; chotchinga chotsatira ndi mzinda wa Yeriko. Yoswa anatumiza azondi awiri mu mzinda wa Yeriko umene unali wotetezedwa kwambiri. Iye ankafuna kudziwa za mzindawu, iye ndi asilikali ake asanapite kukauthira nkhondo. | Yeriko unali mzinda woyamba waukulu mu dziko la Kanani umene Aisrayeli ankayenera kugonjetsa. Yoswa anatuma azondi awiri kuti awoloke Mtsinje wa Yordano kuti akazonde mzindawo ndi kudzamufotokozera iye asanauthire nkhondo. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Azondi analowa mu Yeriko. Mulungu anawatsogolera ku nyumba ya Rahabi. Inali pa malo abwino osavuta kuthawa. Masiku a Yoswa, chinali chizolowezi chomanga nyumba pamwamba pa khoma la mzinda. Mizinda yambiri inali ndi makoma awiri a mamita 3-5 motalikirana. Ankagoneka matabwa pamwamba pa makoma awiriwo ndi kumanga nyumba. Rahabi ankakhala mu nyumba zoterezi zomwe zinkayang'ana kunja kwa khoma. ***(vesi 1-2)***<br>2. Rahabi anali atamva chipambano chachikulu chimene Mulungu anapereka kwa anthu a Israyeli ndipo anatsimikiza kuti Mulungu akuyenera kuti anali Mulungu woona ndipo anakhulupirira ndi kumudalira Iye. ***(vesi 8-11)***<br>3. Nyumba ya Rahabi inali ndi denga la thyathyathya pamene ankaunjika mitengo ya thonje ndipo anali malo abwino obisala azondiwo. Azondi anabisala pamaso pa Mfumu ya Yeriko m'mitengo ya thonje imene inali pa denga la nyumba ya Rahabi ndipo analonjeza kuti adzapulumutsa Rahabi ndi abale ake ngati adzamangirira kansalu kofiira pa zenera la nyumba yake ndiponso ngati abale ake adzakhale ali m'nyumbamo pamene adzathira nkhondo Yeriko. ***(vesi 15-21)***<br>4. Iwo anathawa potsetsereka ndi chingwe kuchokera pa zenera la nyumba ya Rahabi. Atabisala m'mapiri masiku atatu, azondi aja anawoloka Mtsinje wa Yordano ndi kubweretsa nkhani yothandiza kwa Yoswa. ***(vesi 22-24)***<br>5. Onetsetsani kuti ophunzira akumvetsa kuti Rahabi anadzipereka kupulumutsa azondi aja chifukwa cha chikhulupiriro chake mwa Mulungu wawo – Mulungu wa Israyeli.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A - Kuzonda dziko. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Azondi analowa mu Yeriko. Mulungu anawatsogolera ku nyumba ya Rahabi. Inali pa malo abwino osavuta kuthawa. Masiku a Yoswa, chinali chizolowezi chomanga nyumba pamwamba pa khoma la mzinda. Mizinda yambiri inali ndi makoma awiri a mamita 3-5 motalikirana. Ankagoneka matabwa pamwamba pa makoma awiriwo ndi kumanga nyumba. Rahabi ankakhala mu nyumba zoterezi zomwe zinkayang'ana kunja kwa khoma. ***(vesi 1-2)***<br>2. Rahabi anazindikira kuti Mulungu wa Kumwamba ndi wamphamvuzonse, ndipo anakhulupirira Iye. Iye ankadziwa kuti milungu yabodza ya Akanani sikanamupulumutsa, kapena mzinda pa zimene zidzawachitikire. ***(vesi 8-11)***<br>3. Chikhulupiriro chatsopano cha Rahabi chinamupatsa kulimbika mtima kuti awabise azondi aja. Azondi anabisala pamaso pa mfumu ya Yeriko pa mitengo ya thonje imene inali pa denga la nyumba ya Rahabi; koma iye anadzipereka kuwapulumutsa chifukwa anazindikira kuti Mulungu wa Israyeli anali woyenera kumudalira.<br>4. Rahabi anali wokhudzidwa ndi chitetezo cha abale ake pamene Aisrayeli adzawathire nkhondo, koma azondi anapeza njira yoti adzawapulumutse. Iye ankayenera kumanga kansalu kofiira pa zenera. ***(vesi 17-20)***<br>5. Chifukwa cha chikhulupiriro chake, abale ake anapulumutsidwa ndipo m'tsogolo anakhala makolo a Ambuye Yesu. ***(Mateyu 1: 5)*** *Fotokozani momwe Mulungu ankakwaniritsira zolinga zake kudzera mwa Rahabi, mkazi wachilendo!*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kutumiza azondi. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro pogwiritsa ntchito mavesi awa:<br>1) ***Ahebri 11: 31*** (Vesi Yoloweza) – N'chifukwa chiyani Rahabi anapulumutsidwa ku imfa pamene nkhondo ya ku Yeriko inkachitika?<br>2) ***Yakobo 2: 25*** – Kodi Rahabi anaonetsa motani chikhulupiriro chake mwa Mulungu?<br>3) ***Ahebri 11: 6*** – Kodi vesi imeneyi ikutiwuza chiyani za chikhulupiriro? | Bwerezani phunziro pogwiritsa ntchito mavesi awa:<br>1) ***Aroma 5: 5-8*** – Moyo wa Rahabi unali 'wosapembedza' mpaka pamene anakhulupirira Mulungu. Koma ife tonse timatchedwa 'osapembedza' mpaka pamene tabwera kwa Yesu kuti atipulumutse.<br>2) ***Aefeso 2: 6-8*** – Mavesi awa akutsindika kuti chipulumutso chimabwera mwa chikhulupiriro, ndipo sitingachite ntchito zabwino kuti tikafike Kumwamba. Kupulumutsidwa kwa Rahabi kunabwera mwachikhulupiriro.<br>3) ***Yakobo 2: 25-26*** – Chikhulupiriro cha Rahabi chinaonekera mu ntchito zake – iye anabisa azondi, ndipo anafuna kuti abale ake apulumutsidwe. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi inu munakhulupirira ndi kudalira Ambuye Yesu amene analangidwa chifukwa cha tchimo lanu?<br>2. Ngati ndinu Mkhristu, kodi 'ntchito' zanu zimasonyeza kuti ndinu wake wa Ambuye Yesu? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Pa ***Ahebri 11***, Rahabi ndi mmodzi mwa amayi awiri amene alembedwa mu 'Gulu la Chikhulupiriro'. Tikakhulupirira Ambuye kwathunthu, Iye adzatidalitsanso ife. Cholinga cha moyo wathu chikhala 'ndikutaya zonse ndi kukhulupirira Iye' –chimenechi ndiye CHIKHULUPIRIRO! |

| | **C8 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Yoswa**<br>**Mutu – Kuwoloka mtsinje** | **C8 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Yoswa**<br>**Mutu – Kuwoloka Yordano** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yoswa 3: 1-17***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yoswa 3: 5***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu analamula Yoswa kuti atenge Aisrayeli ndi kuwoloka Mtsinje wa Yordano ndipo anamuthandiza kuchita zimenezi – Mulungu akalamula, nthawi zonse amathandizanso.<br>2. Pa umunthu zinali zosatheka kutsogolera gulu lalikulu lotere kuwoloka Mtsinje wa Yordano nthawi imene madzi anali atasefukira. Mulungu anachita chodabwitsa chachikulu. | **Werengani:** ***Yoswa 3: 1-17; 4: 1-24***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yoswa 4: 24***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu analamula Yoswa kuti atenge Aisrayeli ndi kuwoloka Mtsinje wa Yordano ndipo anamuthandiza kuchita zimenezi – Mulungu akalamula, nthawi zonse amathandizanso.<br>2. Mulungu ali ndi mphamvuzonse ndipo amafuna kuonetsa mphamvu yake m'miyoyo yathu pamene akugwira ntchito kudzera mwa ife. |
| **MAWU OYAMBA** | Israyeli ankayenera kukumbutsidwa kuti Mulungu anali pakati pawo pamene ankawoloka Yordano. Iwo sankaona Mulungu koma Bokosi la Chipangano limene linali patsogolo pawo monga chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu ndi mphamvu yake. Nthawi imeneyi anali ansembe amene ananyamula. ***(vesi 3)*** | Fotokozani kuti Mtsinje wa Yordano chinali chotchinga chachikulu pofuna kutenga Aisrayeli kulowa m'Dziko la Malonjezano. Israyeli anapeza Nyanja Yofiira pamene anatuluka mu Aigupto. ***(Eksodo 14)*** Pansi pa utsogoleri wa Mose, Mulungu anapereka njira powuma modabwitsa. Moteronso pansi pa ulamuliro wa Yoswa, Mulungu akuchita chodabwitsa china, ndipo anthu akuwoloka mtsinje mosavuta. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yoswa anasonkhanitsa Aisrayeli kuti awawuze zomwe Mulungu anamulamula ndi kuti analonjeza kuchita zodabwitsa pakati pawo. ***(vesi 1-5)***<br>2. Anthu a ku Kanani anali oyipa kwambiri ndipo Mulungu anafuna kuwathamangitsa m'dzikomo chifukwa sankafuna Aisrayeli kuti atsatire njira zawo zoyipa ndi makhalidwe awo.<br>3. Aisrayeli anali ndi chidwi chofuna kuwoloka Mtsinje wa Yordano koma Mulungu anawapatsa malangizo a momwe angawolokere.<br>4. Mapazi a ansembe ataponda mu Mtsinje wa Yordano chodabwitsa chinachitika. Madzi mu mtsinje anayima mu mzinda wa Adamu (makilomita 16 kumpoto) ndi kuunjikana kumeneko ndipo madzi amene ankayenda onse anakalowa mu Nyanja ya Mchere, kulola Aisrayeli awoloke powuma. ***(vesi 14-17)***<br>5. Fotokoza kwa ophunzira kuti Israyeli anamvera malangizo a Mulungu ndipo chinthu chovuta chimene chinkawatchinga chinachoka. Iwo palibe chimene anachita; Mulungu anachita zonse.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuwoloka mtsinje. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nthawi inakwana yoti awoloke Mtsinje wa Yordano, umene nthawi imeneyi unali utasefukira. Ansembe analangizidwa kuti apite patsogolo atanyamula Bokosi la Chipangano. Ichi chinali chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu ndi mphamvu yake. Aisrayeli ankayenera kutsatira patali. ***(3: 1-4)***<br>2. Mapazi a ansembe ataponda mu Yordano, chodabwitsa chinachitika, madzi anayima ku mtunda pa mzinda wa Adamu ndipo ena otsalawo akatira mu Nyanja ya Mchere. Ansembe anayenda mpaka pakati pa mtsinje ndi kukhala pamenepo mpaka anthu onse atawoloka powuma. ***(3: 14-17)***<br>3. Yehova analamula munthu mmodzi pa fuko lililonse la mafuko khumi ndi awiri anyamule mwala pakati pa mtsinje kuti ikamange chikumbutso cha miyala khumi ndi iwiri pa Giligala, pokumbukira kuti Mulungu anayimitsa madzi a Mtsinje wa Yordano. ***(4: 1-9)***<br>4. Anthu atawoloka, Yoswa anamanga chikumbutso cha miyala khumi ndi iwiri pamalo pamene anayima ansembe aja. Pamene anthu ankawoloka kupita mbali ya kumadzulo pamodzi ndi Bokosi la Chipangano, madzi a mu Mtsinje wa Yordano anayambanso kuyenda. ***(4: 9)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuwoloka Yordano. |
| **KUKUMBUTSANA** | Kumbutsani ophunzira kuti monga Mulungu anagawa madzi pa Nyanja Yofiira kuti Aisrayeli atuluke mu Aigupto ***(Eksodo 14)***, moteronso anagawa madzi a Mtsinje wa Yordano kuti iwo alowe m'Dziko la Malonjezano la Kanani. Kupezeka kwa Mulungu ndi kukhulupirika kwake kwa Aisrayeli zinachititsa kuti ulendo wochokera kwa Aigupto kupita ku Kanani utheke. Mulungu anasankha nthawi imene mtsinje unali utasefukira kuti aonetse mphamvu yake. Izi zinatchukitsa mbiri yawo pakati pa adani awo, ***(vesi 10)*** amene anali ambiri kuposa iwo. | Bwerezani phunziro powerenga – ***Salimo 114***. Kambiranani ***vesi 3*** ndi kufotokoza chimene mlembi akunena pa izi:<br>(1) Kugawikana kwa madzi pa Nyanja Yofiira pamene Mose ndi ana a Israyeli anawoloka koma Aaigupto anamira.<br>(2) Kuyima kwa madzi mu Mtsinje wa Yordano mu phunziro lino. Fotokozani kwa ophunzira kuti panali kusiyana kwa zaka makumi anayi pa zochitika zimenezi. Kodi tikuphunzira chiyani za Mulungu pa zochitika ziwiri zimenezi? |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Aisrayeli anamvera malangizo a Mulungu ndipo Mulungu anawapulumutsa. Ife tikamvera Mawu a Mulungu ndi kulandira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wathu, Iye adzatitsogolera pa moyo wathu ndi kutitenga kupita Kumwamba.<br>2. Ganizirani za 'mitsinje' kapena zovuta za moyo wanu. Kodi phunziro ili likutilimbikitsa motani za momwe tingachitire? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga Aisrayeli analonjezedwa za chipambano akayika Bokosi la Chipangano patsogolo, moteronso Akhristu akuyenera nthawi zonse mwa chikhulupiriro kuyika Ambuye Yesu patsogolo pawo.<br>2. Monga miyala khumi ndi iwiri ija inali chizindikiro cha chipambano cha Aisrayeli, moterenso imfa ya Yesu pa mtanda chidzakhala chizindikiro chamuyaya cha chikondi chake pa ife. |

## C8 – KALASI 3
**Phunziro Lachinayi – Yoswa**
**Mutu – Kumvera Yehova**

**Werengani:** ***Yoswa 6: 1-25***
**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11: 30***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Yoswa anamvera malangizo amene Mulungu anamupatsa ndipo inachititsa kuti agonjetse Yeriko.
2. Ife tikuyenera kudalira Mulungu kuti adzatipatsa chipambano pa moyo wathu ngati tikukhulupirira Ambuye Yesu ndi kudalira Iye nthawi zonse.

### MAWU OYAMBA
Yoswa tsopano ankayenera kutsogolera anthu ku nkhondo yolanda Yeriko mzinda umene unali wotetezeda kwambiri, koma zipata ndi makoma zinasunga anthu amene anali m’katimo kuti aweruzidwe! Iwo sakanatha kuletsa Aisrayeli kulowamo! Mulungu anali ndi chikonzero chopereka Yeriko m’manja mwa Aisrayeli.

### KUTSIRIZA
**Perekani Nkhani ya m’Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Kuwopa Ayuda kunachititsa kuti atseke mzinda wa Yeriko Yoswa ndi gulu lake lankhondo asanafike. ***(6: 1)***
2. Aisrayeli anayenda mozungulira Yeriko kamodzi pa tsiku kwa masiku asanu ndi awiri. Patsogolo panali asilikali azida, kenaka ansembe asanu ndi awiri oyimba malipenga, ndipo pambuyo pawo panali Bokosi la Chipangano. Anthu ankatsatira m’mbuyo koma ankayenera kukhala chete. ***(6: 3-14)***
3. Pa tsiku lachisanu ndi awiri, anayenda kuzungulira mzinda kasanu ndi kawiri ndipo pamene ansembe anayimba malipenga mokweza mawu, Aisrayeli anafuwula kwambiri ndipo makoma a Yeriko anagwa pansi. Iwo tsopano anatha kulowa mu mzinda muja. ***(6: 20)***
4. Iwo ankayenera kuononga chilichonse, anthu pamodzi ndi ziweto zawo, koma ankayenera kupulumutsa Rahabi ndi abale ake chifukwa cha zimene Rahabi anachita poteteza azondi komanso kumvera malangizo awo. ***(6: 22-23)***
5. Pa Vesi Yoloweza, tikuphunzira kuti ndi ‘chikhulupiriro’ mwa Mulungu chimene chinagwetsa makoma, ndipo pa ***Ahebri 11: 31*** tikuphunziranso kuti ndi chikhulupiriro chomwechi chinapulumutsa Rahabi.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kumvera Yehova.

### KUKUMBUTSANA
Bwerezani phunziro polimbikitsa ophunzira kuti akambirane izi:
1. Kodi Yehova anawuza Yoswa chikonzero chotani pa ***3-5***?
2. Kodi chinachitika ndi chiyani pamene ansembe anamvera chikonzero cha Yehova chimene anawuza Yoswa pa ***vesi 20***?
3. Kambiranani momwe za kuti chipambano chinabwera chifukwa cha kumvera chikonzero cha Mulungu pa Aisrayeli.

### KHALANI MOYO UMENEWU
**Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**
1. Kodi ***1 Yohane 5: 4-5*** akunena kuti Akhristu angakhale bwanji moyo wachipambano?
2. Phunziro ili likuphunzitsa chikhulupiriro cha Yoswa mwa Mulungu chinabweretsa chipambano kwa Aisrayeli ndipo chikhulupiriro cha Rahabi mwa Mulungu chinamupulumutsa ku imfa. Ngati ife tikhulupirira Ambuye Yesu, Iye adzatithandiza kupambana m’miyoyo yathu.

## C8 – KALASI 4
**Phunziro Lachinayi – Yoswa**
**Mutu – Kugonjetsa ndi kugonjetsedwa**

**Werengani:** ***Yoswa 6: 1-27; 7: 1-26***
**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11: 30***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Yoswa anamvera malangizo amene Mulungu anamupatsa ndipo inachititsa kuti agonjetse Yeriko. Koma kusamvera kwa Akani kunachititsa kuti agonjetsedwa ku Ai.
2. Kukhulupirira Mulungu ndi kumvera Iye zimabweretsa mtendere, chimwemwe ndi chisangalalo m’moyo uno ndi ku moyo wamuyaya. Tchimo komanso kusamvera Mulungu zimakhala ndi zotsatira zoyipa kwambiri pa moyo wathu.

### MAWU OYAMBA
Tsopano Aisrayeli ali m’Dziko la Malonjezano anakumana ndi zotchinga ziwiri. Mizinda ya Yeriko ndi Ai linali phunziro lofunika kwambiri kwa Aisrayeli pamene ankayamba kutenga dziko la Kanani. Iwo akadalira Mulungu ndi kumumvera kwathunthu, akulonjezedwa chipambano. Koma akapanda kumvera Mulungu ndi kudzidalira okha, adzagonjetsedwa.

### KUTSIRIZA
**Perekani Nkhani ya m’Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Ngakhale Mulungu anawuza Yoswa kuti nthawi yakwana kuti atenge Yeriko, Iye anamupatsa malangizo a kachitidwe ka nkhondo, kumukumbutsa kuti chipambano chidzachokera kwa Mulungu yekha. Yeriko unali mzinda woyipa ndipo ankayenera kuwononga. ***(6: 2-5)***
2. Aisrayeli anayenda mozungulira Yeriko kamodzi pa tsiku kwa masiku asanu ndi awiri. Patsogolo panali asilikali azida, kenaka ansembe asanu ndi awiri oyimba malipenga, ndipo pambuyo pawo panali Bokosi la Chipangano. Anthu ankatsatira m’mbuyo koma ankayenera kukhala chete. ***(6: 3-14)*** Panali malangizo apadera a tsiku lachisanu ndi chiwiri. ***(6: 15-17)***
3. Rahabi ndi abale ake anapulumuka ku chionongeko chifukwa anali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu komanso anabisa azondi aja amene anatumizidwa kukaona Yeriko. ***(6: 22-23)***
4. Yoswa ndi ankhondo anadabwa pamene anagonjetsedwa ndi kamzinda kakang’ono ka Ai pamene iwo anagonjetsa modabwitsa Yeriko. Pasanathe nthawi Yoswa anazindikira kuti linali tchimo mu msasa mwawo limene linachititsa izi. ***(7: 6-12)***
5. Akani sanamvere Mulungu potenga zinthu za adani zomwe zinali zodetsedwa monga mmene Mulungu analamulira kuti chilichonse cha mu Yeriko chikuyenera kuonongedwa. ***(6: 18-19 ndi 7: 11-12)***
6. Akani anavomereza tchimo lake ndipo iye pamodzi ndi banja lake lonse anawagenda miyala ndi kuwapha ndi cholinga chakuti tchimo lake lisapezeke m’dziko la Kanani. ***(7: 20-26)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kugonjetsa ndi kungonjetsedwa.

### KUKUMBUTSANA
1. Werengani ***Yakobo 1: 12-16*** ndi kukambirana za kuti (1) ***vesi 12*** ikukhudza Rahabi; (2) ***vesi 13-15*** ikukhudza Akani; ndi (3) ***vesi 12-16*** akukhudza ife tonse.
2. Kambiranani za kuti tchimo la Akani linali ndi zotsatira zoyipa kwambiri pa banja lake komanso kwa asilikali anzake, kufotokoza kuti cholakwa chimodzi chimabala china.

### KHALANI MOYO UMENEWU
**Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**
Ngakhale kuti anthu osamvera amabweretsa chisoni m’miyoyo yawo, komanso miyoyo ya ena, anthu omvera amabweretsa chisangalalo ndi madalitso m’miyoyo yawo. Ngati ndinu Mkhristu, kodi mumaonetsa motani m’moyo mwanu kumvera kwanu Mulungu? Pamene Yoswa anapita kukachita nkhondo ndi Ai, iye sanafunse Mulungu. Kodi zotsatira zingakhale zotani kwa Akhristu ngati nthawi zonse amadalira mphamvu zawo? Kodi tikuphunzira chiyani mu phunziro la lero?

| | **C9 – KALASI 3**<br>**Phunziro Loyamba – Eliya**<br>**Mutu – Kulamulidwa ndi Mulungu** | **C9 – KALASI 4**<br>**Phunziro Loyamba – Eliya**<br>**Mutu – Chilango cha Mulungu** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Mafumu 16: 29-33; 17: 1-7***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 17: 5***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Nthawi zonse Aisrayeli akamadutsa m'mavuto, Mulungu ankakhala ndi munthu woyankhula m'malo mwake.<br>2. Eliya anali munthu amene Mulungu anamusankha kuti ayankhule zotsutsa Mfumu Ahabu ndi zoyipa zake zonse. | **Werengani:** ***1 Mafumu 16: 29-33; 17: 1-7***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 17: 5***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Nthawi zonse Aisrayeli akamadutsa m'mavuto, Mulungu ankakhala ndi munthu woyankhula m'malo mwake. Eliya anali munthu amene Mulungu anamusankha kuti ayankhule zotsutsa Mfumu Ahabu ndi zoyipa zake zonse.<br>2. Kumvera Mulungu ndi Mawu ake ndi chinthu chofunika kwambiri pa miyoyo yathu pa dziko lapansi. |
| **MAWU OYAMBA** | M'maphunziro awa, tikuwuzidwa za Eliya, mmodzi mwa aneneri aakulu mu Israyeli. Eliya ankakhala nthawi imene Mfumu Ahabu ankalamulira Israyeli. Ahabu anali mfumu yoyipa kwambiri, ndipo anakwatira mkazi amene anali woyipa kwambiri kuposa iye, wotchedwa Yezebeli. Yezebeli ankapembedza fano lotchedwa Baala ndipo anakopa mwamuna wake kuti alimbikitse kupembedza fanoli nthawi imeneyo. Aisrayeli anatembenuka kusiya Mulungu mmodzi ndi woona. | Eliya anali woyamba pa m'ndandanda wa aneneri a Mulungu ofunika kwambiri amene Mulungu anawatuma ku Israyeli (Ufumu wa Kumpoto) ndi Yuda (Ufumu wa Kummwera). Mulungu ankayitana aneneri kuti adzapulumutse Israyeli ku moyo oyipa ndi makhalidwe oyipa. Kwa zake 300, abambo ndi amayi amenewa ankalimbikitsa anthu ndi atsogoleri awo kuti abwerere kwa Mulungu yekha woona. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ahabu anali woyipa kwambiri kuposa mfumu ina iliyonse imene inakhalapo. ***(1 Mafumu 16: 30 -33)***<br>2. Mulungu anatuma Eliya kuti akatsutse anthu a Israyeli chifukwa cha kupembedza mafano ndi miyoyo yawo ya uchimo ndi kuwalimbikitsa kuti atembenuke mtima.<br>3. Eliya molimba mtima analengeza kwa Ahabu kuti kudzakhala chilala ndipo mvula sibwera kwa zake zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi. ***(Yakobo 5: 17)*** Ichi chinali chilango cha Mulungu chifukwa cha kupembedza mafano. ***(17: 1)***<br>4. Mulungu anawuza Eliya kuti achoke ku Samariya ndi kupita kummawa ku mtsinje wa Keriti kumene akhwangwala adzamudyetsa ndipo adzamwa madzi a mtsinje. Koma patapita nthawi pang'ono madzi mu mtsinjemo anawuma. ***(17: 2-7)***<br>5. Eliya anakhulupirira mawu a Mulungu ndi kumvera malangizo, motero Mulungu anakwaniritsa zosowa zake zonse.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kulamulidwa ndi Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mkazi woyipa wa Ahabu, Yezebeli, anachokera ku mzinda wa Fonike ku Turo kumene abambo ake, Etibaala, anali mkulu wa ansembe ndi mfumu. Yezebeli ankapembedza Baala ndipo pofuna kumukondweretsa, Ahabu anamanga guwa lansembe la Baala. ***(1 Mafumu 16: 30-33)*** Izi zinalimbikitsa mafano ndipo zinatsogolera dziko la Israyeli ku tchimo.<br>2. Opembedza Baala ankakhulupirira kuti anali Baala amene ankabweretsa mvula ndi zokolola zabwino. Pamene Eliya molimba mtima anawuza Ahabu kuti mvula sibwera zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi, ***(Yakobo 5: 17)*** Ahabu anadabwa kwambiri. ***(17: 1)***<br>3. Eliya anawuza Ahabu za mphamvu yoposa mulungu wachikunja wina – 'Yehova Mulungu wa Israyeli'. ***(1 Mafumu 17: 1)***<br>4. Nthawi imene kuwukira ndi kupembedza mafano kunafika pa chimake mu Israyeli, Mulungu analowerera potumiza chilala. Koma, Iye anawuza Eliya kuti achoke mu Samariya ndi kupita kummawa kwa Mtsinje wa Yordano ku Mtsinje wa Keriti. Kumeneko azikamwa madzi a mu mtsinje ndipo akhwangwala azikabweretsa chakudya. ***(17: 2-6)***<br>5. Eliya anakhulupirira mawu a Mulungu ndi kumvera malangizo, motero Mulungu anakwaniritsa zosowa zake zonse.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Chilango cha Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Funsani ophunzira kuti alembe izi mwachidule m'mawu awo:<br>(i) Mbiri ya zomwe zinkachitika mu phunziro lino.<br>(ii) Uneneri wa Eliya kwa Ahabu.<br>(iii) Lonjezo la Mulungu kwa Eliya. | 1) Werengani ***Deuteronomo 4: 23*** ndi kukambirana momwe vesi iyi ikukhudzira Mfumu Ahabu. Werengani ***Deuteronomo 7: 1-6*** ndi kukambirana za kuti Mulungu anawuza Aisrayeli kuti asakwatirane kapena kukhala pa ubale ndi adani a Mulungu. Mulungu akuwachenjeza kuti ubale wotero udzachititsa anthu ake atembenuke ndi kusiya Mulungu woona.<br>2) Werengani ***vesi 6*** ndi kukambirana momwe Mulungu ankaonera kuti Israyeli anali 'anthu ake apadera'. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ndi chifuniro cha Mulungu kuti tilape tchimo lathu, ndipo padzakhala zotsatira zake ngati tipitiriza kukhala moyo wauchimo.<br>2. Monga zinatengera kulimba mtima kuti Eliya awuze munthu woyipa, Ahabu, kuti kudzakhala chilango chifukwa cha tchimo lawo, moteronso zimatengera kulimba mtima kuti munthu akhale moyo wa Chikhristu pamene ambiri amene tikumadziwana nawo sadziwa Ambuye monga Mpulumutsi wawo. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Eliya anali mboni yamphamvu ya Mulungu mu nthawi yoyipa kwambiri. Iye analozera anthu kwa Yehova. Kodi Akhristu angatsatire motani chitsanzo chake (onani ***Luka 1: 17***)?<br>2. Eliya ankadziwika kuti anali munthu wa Mulungu komanso chifukwa cha kumvera Mulungu kwake. N'chifukwa chiyani kumvera Mulungu chikuyenera kukhala chinthu choyamba m'miyoyo yathu? |

| | C9 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Eliya<br>Mutu – Kusamalidwa ndi Mulungu | C9 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Eliya<br>Mutu – Chisamaliro cha Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Mafumu 17: 7-24***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 17: 24***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngakhale kunali chilala chachikulu, Mulungu anasamalira Eliya.<br>2. Amene amatenga Mulungu kukhala woyamba sadzasowa zinthu zofunika pa moyo wawo. | **Werengani:** ***1 Mafumu 17: 7-24***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 17: 24***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu amakwaniritsa malonjezo ake.<br>2. Mulungu amalonjeza moyo wosatha tikakhulupirira Mwana wake monga Mpulumutsi wathu, ndipo atha kutipanga ife kukhala abambo ndi amayi a Mulungu. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira phunziro la m'mbuyo zomwe zinachitika nthawi ya chilala. Mulungu ankasamalira Eliya koma tsopano madzi a mu mtsinje wa Keriti anawuma. Mulungu sanayiwale Eliya koma anamuwuza kuti apite ku Zarefati. Mudzi wa Zarefati unali m'mbali mwa Nyanja Yayikulu, pakati pa mizinda ya Turo ndi Sidoni, ulendo wautali ndithu. | Kumbutsani ophunzira phunziro la m'mbuyo. Mulungu tsopano walamula Eliya kuti apite ku Zarefati chifukwa madzi awuma mu mtsinje wa Keriti. M'phunziro lino tiphunzira zoti Eliya anapita kwa mayi wamasiye wa Amitundu kuti akapeze thandizo ndipo, zotsatira zake, mayiyo anadalitsika kuposa mmene ankayembekezera! |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Momvera Mulungu Eliya ananyamuka kupita ku Zarefati pakuti Mulungu anali atakonza kuti mayi wamasiye wa Amitundu akasamalire Eliya. ***(17: 7-9)***<br>2. Eliya atakumana ndi mayiyu, iye anapempha kuti amupatse buledi koma mayiyo anakana popeza anali ndi ufa okwanira mwana wake ndi iyeyo. Eliya anati Mulungu adzaonetsetsa kuti ufa ndi mafuta zisathe. Mayi wamasiyeyo anamvera ndipo ufa sunathe mpaka chilala chitatha. ***(17: 10-16)***<br>3. Pambuyo pake, mwana wa mayiyo anadwala ndi kumwalira. Eliya anapemphera kwa Mulungu kuti mwanayo akhalenso moyo, ndipo Mulungu anayankha pemphero lake. Iye anapereka mwanayo kwa amayi ake ali moyo. ***(17: 17-23)***<br>4. Mayi wamasiye wa ku Zarefati anavomereza kuti Eliya anali 'munthu wa Mulungu'. ***(17: 24)***<br>5. Mulungu anagwiritsa ntchito akhwangwala, mbalame zodetsedwa, ndi mayi wamasiye wosauka kukwaniritsa zosowa za Eliya. Mulungu amakhala ndi thandizo kuchokera kumene sitimakuyembekezera ndi kupereka kwa ana ake m'njira imene imaposa maganizo athu. ***(Onani Mateyu 6: 25-34)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kusamalidwa ndi Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Momvera Mulungu Eliya akupita ku Zarefati kumene mayi wamasiye wa Amitundu akukonza chimene akukhulupirira kuti ndi chakudya chomaliza cha iye ndi mwana wake. ***(17: 7-12)***<br>2. Eliya akumuwuza kuti poyamba apange buledi wake ngakhale ali ndi chakudya chochepa. Iye anakhulupirira Eliya ndipo potero anatenga Mulungu kukhala woyamba, ndipo ufa sunathe m'dengu ndi mafuta ake sanathe m'botolo. ***(17: 12-16)***<br>3. Patapita nthawi mwana wake uja anadwala ndi kumwalira. Eliya ananyamula mwanayo kupita naye ku chipinda chake, anamukhumbatira katatu ndi kupemphera kwa Yehova kuti amaukitse. Mnyamatayo anatsitsimuka ndipo anapita naye kwa amayi ake ali wamoyo ndi wathanzi. ***(17: 17-23)***<br>4. Mayi wamasiye wa Amitundu uyu anatsimikizika kwathunthu, popanda kukayikiranso chifukwa cha zodabwitsa zimenezi kuti Eliya anali munthu wa Mulungu, ndi kuti mawu a Yehova anali woona – osati mafano amene ankalimbikitsa Ahabu ndi Yezebeli. ***(17: 24)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Chisamaliro cha Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro ili pofunsa ophunzira mafunso amene adzawathandiza kulemba mayankho a mafunso mu Phunziro 2. | 1. Werengani ***Mateyu 6: 31-34*** ndi kukambirana momwe ***vesi 33*** ikukhudzira zomwe zinachitika kwa mayi wamasiye wa Amitundu.<br>2. Werengani ***Ahebri 11: 32-35*** ndipo onetsani ***vesi 35*** kuti ikunena mayi wamasiye wa ku Zarefati ngati mmodzi mwa anthuwo. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Moyo wa Eliya unali moyo wa pemphero. Iye ankakhulupirira kuti adzalandira chimene wapemphera. Pamene tipemphera, kodi timakhulupirira kuti Mulungu ayankha?<br>2. Eliya anali womvera Mulungu ndipo ankalandira zosowa zake. Ife tikuyenera kumvera Mulungu powerenga Baibulo ndi kupemphera kuti azititsogolera.<br>3. Eliya ankadziwika kuti anali 'munthu wa Mulungu'. Kambiranani kuti zimatanthauza chiyani. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Mayi wamasiye anakhulupirira Mawu a Mulungu ndipo anadalitsika kwambiri. Kodi pa nkhani imeneyi tikuphunzira chiyani?<br>2. Eliya anali munthu wa Mulungu amene anamvera Mulungu ndipo zosowa zake zinkakwaniritsidwa ngakhale ankakhala mu nthawi yovuta. Kodi Mulungu amadalitsabe anthu lero amene akukumana ndi zinthu zovuta pa moyo wawo? |

| | C9 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Eliya<br>Mutu – Kutsutsana ndi aneneri a Baala | C9 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Eliya<br>Mutu – Mphamvu ya Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Mafumu 18: 1-2, 16-46***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 18: 39***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Eliya anaonetsa pa Phiri la Karimeli kuti Mulungu wake ndi Mulungu woona.<br>2. Pali Mulungu mmodzi yekha woona ndipo ndi Iye yekha amene amayankha mapemphero anthu. Iye anapereka Mwana wake, Ambuye Yesu, kukhala Mpulumutsi wathu. | **Werengani:** ***1 Mafumu 18: 1-46***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yakobo 5: 17-18***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Eliya anaonetsa pa Phiri la Karimeli kuti Mulungu wake ndi Mulungu woona.<br>2. Mulungu amamva ndi kuyankha mapemphero a Akhristu amene amakhala moyo womvera ndi wokhulupirika kwa Iye. |
| **MAWU OYAMBA** | Mulungu analamula Eliya kuti akaonekere pamaso pa Mfumu Ahabu. Tsiku lina Eliya anakumana ndi Obadiya, nduna ya Mfumu Ahabu ndi kumuwuza kuti akonze msonkhano woti akumane ndi Mfumu Ahabu. Eliya anawuza Ahabu kuti asonkhanitse mafano ake pa Phiri la Karimeli kuti akaone Mulungu woona ndi uti. Eliya anaonetsa kulimba mtima nthawi imeneyi pakuti Mfumu Ahabu ndi mkazi wake ankadana naye. | Nthawi ya Eliya kunali aneneri ambiri onyenga amene ankatchinga kuti Mawu a Mulungu asapite kwa anthu. Iwo ankabweretsa uthenga umene unali otsutsana ndi mawu a aneneri woona. Iwo ankalalikira 'uthenga' umene unkalimbikitsa makhalidwe a uchimo a anthu komanso ankayankhula zokhazo zimene anthu ankafuna kumva. Aneneri woona monga Eliya ankayankhula choonadi cha Mulungu. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Gulu lalikulu la anthu litasonkhana pa Phiri la Karimeli, Eliya anadzudzula anthu a Israyeli chifukwa cha kusakhazikika pa chimodzi. Iye anawalangiza kuti akuyenera kusankha pakati pa Mulungu ndi Baala. Choncho anakonza mpikisano kuti adziwe Mulungu woona ndi uti. ***(18: 21)***<br>2. Anapereka nsembe ng'ombe ziwiri, imodzi ya aneneri a Baala ndipo inayo ya Eliya, ndipo Mulungu amene ayankhe pobweretsa moto ndiye Mulungu woona. Aneneri 850 anafuulira kwa mulungu wawo tsiku lonse koma sanayankhe. ***(18: 22-29)***<br>3. Eliya anakonzanso guwa lansembe la miyala khumi ndi iwiri ndipo anayikapo nsembe yake. Iye anathira madzi paliponse. Kenaka anapemphera kwa Mulungu kuti atumize moto kuchokera Kumwamba. Nthawi yomweyo izi zinachitika ndipo anthu anavomereza kuti Mulungu wa Eliya ndi Mulungu woona. Aneneri onse a Baala anaphedwa. ***(18: 30-40)***<br>4. Eliya anawuza Ahabu kuti adye asanabwerere ku Yezreeli chifukwa mvula inali pafupi kubwera ndipo ankayenera kutsika pa Phiri la Karimeli. Eliya ankathamanga patsogolo pa gareta la Ahabu kusonyeza kukhulupirika kuti anali pansi pa ulamuliro wa Ahabu ngakhale Ahabu ankamuda Eliya. ***(18: 41-46)***<br>5. Fotokozani kuti ifenso tikuyenera kusiya milingu yathu yabodza ndi kukhulupirira Mulungu woona ndi wamoyo.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kutsutsana ndi aneneri a Baala. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu anawuza Eliya kuti akaonekera pamaso pa Ahabu ndipo iye anakumana ndi Obadiya, nduna ya Ahabu. Obadiya anali wokhulupirira wokhulupirika ndipo anawuza Eliya kuti Ahabu ankafunafuna Eliya. Eliya anawuza Obadiya kuti akawuze Mfumu Ahabu kuti akufuna kuonana naye. ***(18: 3-15)***<br>2. Eliya atakumana ndi Ahabu anamuwuza kuti sankamvera malamulo a Mulungu koma ankatsogolera Israyeli kupembedza mafano. Eliya anabweretsa maganizo akuti pakhale mpikisano pakati pa iye ndi aneneri onyenga 850 a Baala kuti aone Mulungu woona ndi uti. ***(18: 18-19)***<br>3. Anapereka nsembe ng'ombe ziwiri, imodzi ya aneneri a Baala ndipo inayo ya Eliya, ndipo Mulungu amene ayankhe pobweretsa moto ndiye Mulungu woona. Aneneri 850 anafuulira kwa mulungu wawo tsiku lonse koma sanayankhe. ***(18: 22-29)***<br>4. Eliya anakonzanso guwa lansembe la miyala khumi ndi iwiri ndipo anayikapo nsembe yake. Iye anathira madzi paliponse. Kenaka anapemphera kwa Mulungu kuti atumize moto kuchokera Kumwamba. Nthawi yomweyo izi zinachitika ndipo anthu anavomereza kuti Mulungu wa Eliya ndi Mulungu woona. Aneneri onse a Baala anaphedwa. ***(18: 30-41)***<br>5. Eliya anapemphera kuti mvula ibwere ndipo anapitiriza kupemphera mpaka mtambo unaoneka. Iye anawuza Ahabu kuti abwerere ku nyumba yake yaufumu ku Yezreeli msangamsanga ndipo iye ankathamanga patsogolo pa gareta lake atanyowa ndi mvula. Mulungu anachita chodabwitsa kugonjetsa aneneri a Baala. ***(18: 41-46)***<br>6. *Fotokozani kuti ifenso tikuyenera kusiya milungu yabodza ndi kukhulupirira Mulungu woona ndi wamoyo. Ngati wina wake kapena china chake chitenga malo a Mulungu m'moyo wathu, ndiye kuti tikutsatira mulungu wabodza.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B –Mphamvu ya Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro pofunsa ana kuti ayankhe mafunso awa:<br>a) Kodi Mulungu anawuza Eliya kuti achite chiyani ***(vesi 1)***?<br>b) Kodi Obadiya ankachita chiyani pamene ankakumana ndi Eliya?<br>c) Kodi Eliya anawuza chiyani Ahabu zoti achite pofuna kudziwa kuti Mulungu woona ndi uti?<br>d) Kodi Mulungu anayankha motani mapemphero a Eliya? | Werengani ***Yoswa 24: 15*** ndipo fananitsani ndi ***1 Mafumu 18: 21***. Kambiranani momwe Yoswa ndi Eliya analimbikitsira anthu kuti akhale mbali ya Mulungu ndi kuti palibe chinthu monga 'kutengekatengeka' pa moyo.<br>Werengani ***Yesaya 45: 21-22*** ndi kukambirana zomwe mavesi akunena za Mulungu woona yekha. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Eliya ankakhulupirira Mulungu ndipo sankaopa kukhala mbali yake. Monga Akhristu, tikuyenera kukhala mbali ya Mulungu ngakhale pamene ena akumukana.<br>2. Eliya anapemphera mu nthawi ya mavuto akulu kwa Mulungu woona ndipo mapemphero ake anayankhidwa. Ife tikuyenera kutsatira chitsanzo chake. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Anthu mu nthawi ya Eliya ankayenera kusankha kumvera Mulungu kapena mafano. Ife tikuyenera kusankha amene tidzamumvera, ndiponso ngati muli zinthu m'miyoyo yathu zomwe zimatenga malo a Mulungu.<br>2. Ngati tasankha kumvera Mulungu, tiyesetse kukhala moyo omvera Mawu ake tsiku ndi tsiku. |

| | **C9 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Eliya**<br>**Mutu – Kusokonekera chifukwa cha mantha** | **C9 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Eliya**<br>**Mutu– Kupezeka kwa Mulungu** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Mafumu 19: 1-18***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 19: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Eliya atapambana, tsopano chikhulupiriro chake chikuyesedwa ndipo akudutsa mu nyengo yovuta.<br>2. Ife tisamalole mantha ndi nkhawa kulowa m'malo mwa chikhulupiriro chathu mu Mulungu, chifukwa Mulungu angathe kutithandiza kugonjetsa mavuto athu onse ndi cholinga chakuti tikhalebe ofunika pa ntchito yake. | **Werengani:** ***1 Mafumu 19: 1-18***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yakobo 4: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Eliya atapambana, tsopano chikhulupiriro chake chikuyesedwa ndipo akudutsa mu nyengo yovuta.<br>2. Pamene takhumudwa ndi kusautsika mu mtima, Mulungu amamvetsetse ndipo tikuyenera kumupempha kuti atithandize. |
| **MAWU OYAMBA** | M'maphunziro a m'mbuyo, taphunzira kuti Eliya analosera za kuyamba ndi kutha kwa zaka zitatu za chilala. Iye anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kupereka wamoyo mwana amene anafa kwa amayi. Iye anayimiranso Mulungu pa mpikisano ndi ansembe a Baala. Ngakhale anachita zonsezi, Eliya anachita mantha ndi kusautsika m'maganizo pameneYezebeli anamuopseza chifukwa cholamula kuti aneneri ake aphedwe. | Yezebeli anakwiya kwambiri chifukwa cha kuphedwa kwa aneneri ake. Eliya, amene anachititsa kuti aneneri ake aphedwe, anali 'chimbayo m'thiti mwake' chifukwa nthawi zonse ankanenera za chionongeko ndi mdima. Popeza Yezebeli sakanatha kuletsa zochita za Eliya, iye anafuna kupha Eliya, motero iye anathawa kufuna kupulumutsa moyo wake. Ngati Eliya anali ndi moyo, Yezebeli sakanatha kuchita zoyipa zonse zimene ankafuna. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Eliya anathawa Yezebeli ndi kupita ku Beereseba ku chipululu ndipo anakhala pansi pa mtengo wa thundu kufuna atangofa. ***(19: 1-5)***<br>2. Mulungu anamuthandiza kuti apume pomupatsa chakudya ndi madzi akumwa ndipo kenaka iye anayenda masiku makumi anayi kuchokera ku Beereseba kupita ku phanga la pa Phiri la Sinai (Horebu). ***(19: 5-9)***<br>3. Mulungu anamufunsa chomwe ankachita kumeneko. Eliya anati iye watsala yekha pamaso pa Mulungu woona. Ana a Israyeli onse akupembedza mafano. Mulungu anawuza Eliya kuti ayime pa khomo la phanga pamene anakhala usiku wonse. ***(19: 9-11)***<br>4. Mulungu anafika pa phiripo ndi mphepo, chivomerezi ndi moto. Moto utadutsa, Eliya anamva mamwu onong'ona ndipo Mulungu anayankhula naye. ***(19: 11-14)***<br>5. Yehova anamuwuza kuti apite kumpoto ku Chipululu cha Damasiko kumene akadzoze anthu atatu. Ngakhale anali ndi mantha, Mulungu anamupatsa Eliya ntchito yofunika kuti agwire. Iye ankayenera kudzoza (i) Hazaeli kukhala mfumu ya Suria; (ii) Yehu kukhala mfumu ya Israyeli; ndi (iii) Elisa kulowa m'malo mwake. ***(19: 15-18)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kusokonekera chifukwa cha mantha. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Eliya atapambana pa nkhondo za uzimu, anayamba kukhumudwa ndi kusautsika m'maganizo. Iye anathawira ku chipululu ku Beereseba. ***(19: 1-5)***<br>2. Mulungu anamusamalira pomupatsa chakudya ndi madzi akumwa. Eliya anapita ku Phiri la Sinai (Horebu) atadya koma akuganiza kuti watsala yekha amene ali ndi Mulungu woona. Iye anayiwala kuti analipo ena amene analinso okhulupirika, mu nthawi imene m'dziko munali zoyipa. Mu Israyeli munali anthu 7,000 amene sanagwadire Baala. ***(19: 5-9 ndi 18)***<br>3. Mulungu anawuza Eliya kuti ayime pa khomo la phanga pamene anakhala usiku wonse. ***(19: 9-11)***<br>4. Mulungu anafika pa phiripo ndi mphepo, chivomerezi ndi moto. Moto utadutsa, Eliya anamva mawu onong'ona ndipo Mulungu anayankhula naye. ***(19: 11-14)***<br>5. Yehova amamuwuza kuti apite kumpoto ku Chipululu cha Damasiko kumene akadzoze anthu atatu. Ngakhale anali ndi mantha, Mulungu anamupatsa Eliya ntchito yofunika kuti agwire. Iye ankayenera kudzoza (i) Hazaeli kukhala mfumu Suria; (ii) Yehu kukhala mfumu ya Israyeli; ndi (iii) Elisa kulowa m'malo mwake. ***(19: 15-18)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kupezeka kwa Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro pofuna ophunzira kuti anene mwachidule, m'mawu awo:<br>a) Kodi Yezebeli anapseza chiyani?<br>b) Fotokozani zomwe zinamuchitikira Eliya pa Phiri la Sinai.<br>c) Kodi ndi ntchito ziti zofunika zimene Mulungu anamutuma? | 1) Werengani ***Yesaya 40: 29-31*** ndi kukambirana ndi ophunzira momwe mavesi amenewa akufotokozera za zomwe zinachitikira Eliya poyamba ndi pomaliza pa phunziro lino.<br>2) Werengani ***Ahebri 13: 5-6*** ndi kukambirana ndi ophunzira kuti, m'malo mwa kukhumudwa ndi kusautsika m'maganizo, Eliya akanadalira Mulungu kuti akwaniritsa zosowa zake zonse. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ngati ndinu wokhulupirira Ambuye Yesu Khristu, simuli nokha chifukwa Ambuye amakhala nanu nthawi zonse. Onani ***Salimo 56: 3***.<br>2. Ngakhale tili ndi zolephera ndi zofooka, Ambuye angathe kutipanga ife kukhala antchito ake ofunika. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Pamene takhumudwa, nthawi zonse tikuyenera kukumbukira kuti Ambuye samatiyiwala ngati tili mbali yake.<br>2. Mulungu amatiyankhula kudzera m'Baibulo nthawi zambiri 'potinong'oneza' kuposa mu 'kufuula' monga mmene taona kale mu phunziro lathu. Kodi izi zikutanthauza chiyani pa zochitika pa moyo wa Mkhristu? |

| | C10 – KALASI 3<br>Phunziro Loyamba – Elisa<br>Mutu – Eliya akumana ndi Elisa | C10 – KALASI 4<br>Phunziro Loyamba – Elisa<br>Mutu – Elisa ndi Eliya |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Mafumu 19: 19-21, 2 Mafumu 2: 1-15***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 19: 21***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ntchito ya Eliya tsopano inatha; inali nthawi yoti iye achoke ndipo Elisa alowe m'malo mwake.<br>2. Monga ngati Elisa amene ankafuna 'magawo awiri' a Eliya potumikira Mulungu monga iye, ifenso tikuyenera kutsanzira Yesu Khristu mmene tingathere. | **Werengani:** ***1 Mafumu 19: 19-21, 2 Mafumu 2: 1-22***<br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 2: 14***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ntchito ya Eliya tsopano inatha; inali nthawi yoti iye achoke ndipo Elisa alowe m'malo mwake.<br>2. Monga ngati Elisa amene ankafuna 'magawo awiri' a Eliya potumikira Mulungu monga iye, ifenso tikuyenera kutsanzira Yesu Khristu mmene tingathere. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira za C9 Phunziro 4 za malangizo a Mulungu kwa Eliya. Nthawi inakwana kuti Eliya atsirize ntchito ya Mulungu pa dziko lapansi ndipo Elisa ndiye akuyenera kulowa m'malo mwake. Iwo anayenera kugwira ntchito pamodzi kwa kanthawi ndipo kenaka Mulungu anali ndi chikonzero chotenga Eliya kupita naye Kumwamba. | Kumbutsani ophunzira za C9 Phunziro 4 za malangizo a Mulungu kwa Eliya. Nthawi inakwana kuti Eliya atsirize ntchito ya Mulungu pa dziko lapansi ndipo Elisa ndiye akuyenera kulowa m'malo mwake. Iwo anayenera kugwira ntchito pamodzi kwa kanthawi ndipo kenaka Mulungu anali ndi chikonzero chotenga Eliya kupita naye Kumwamba. Pali zambiri zofanana mu utumiki wa Eliya ndi Elisa. Koma ngakhale Elisa anachita zodabwitsa zambiri ndi kuwuza Israyeli kuti abwerere kwa Mulungu, iwo anakakamira kukhala moyo wauchimo ndi oyipa. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Eliya anachita monga mmene analamulidwa. Iye anayitana Elisa kuti azimutsata ndipo anakhala mtumiki wake kwa zaka zambiri. ***(19: 19-21)***<br>2. Kenaka nthawi inakwana yoti Eliya achoke. Eliya asanachoke, anapita ku malo anayi: Giligala, Beteli, Yeriko ndi Yordano, ndipo Elisa anakakamira zopita ku malo onsewa ndi Eliya. ***(2 Mafumu 2: 1-7)***<br>3. Kenaka iwo anafika ku Mtsinje wa Yordano. Eliya anamenya madzi a Mtsinje wa Yordano ndi chofunda chake, madzi anagawikana ndipo onse awiri anawoloka powuma. Elisa anapempha 'magawo awiri' a mzimu wa Eliya, kusonyeza kuti ankafuna kukhala ngati amene walowa m'malo mwake. ***(2 Mafumu 2: 8-10)***<br>4. Iwo akuyenda, anasiyanitsidwa ndi gareta ndi akavalo amoto ndipo Eliya anatengedwa kupita Kumwamba mu kamvuluvulu. ***(2 Mafumu 2: 11-13)***<br>5. Ali ndi chisoni, Elisa anabwerera ku Mtsinje wa Yordano ndipo anamenya madzi ndi chofunda chimene Eliya anachisiya. Madzi anagawikananso ndipo anawoloka powuma. Ana a aneneri atawona kuti madzi a mu Yordano agawikana, anamvetsetsa kuti Elisa ndiye anali wolowam'malo weniweni wa Eliya. ***(2 Mafumu 2: 13-15)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Eliya akumana ndi Elisa. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Eliya watsala pang'ono kutengedwa kupita Kumwamba ndipo anapereka udindo kwa Elisa pomuponyera chofunda chake pa mapewa ake. Chofunda chinali chinthu chofunika kwambiri chimene munthu ankayenera kukhala nacho masiku amenewo. Elisa anapha ng'ombe, kuonetsa kuti asabwereranso ku moyo wa mlimi wachuma ndipo anatsanzika makolo ake. ***(1 Mafumu 19: 19-21)***<br>2. Nthawi inakwana yoti Eliya atsirize utumiki wake ndipo anapita ku Giligala, Beteli, Yeriko ndi ku Yordano komaliza. Elisa anamutsatira mokhulupirika popita naye ku malo onsewa. Eliya anamenya Mtsinje wa Yordano ndi chofunda chake, madzi anagawikana ndipo onse anawoloka powuma. Ndi kumeneku kumene Elisa anapempha 'magawo awiri' a mzimu wa Eliya, chimene Mulungu anamupatsa. Eliya anatengedwa kupita Kumwamba. ***(2 Mafumu 2: 1-12)***<br>3. Elisa anawolokanso Yordano ndipo anagwiritsa ntchito chofunda cha Eliya kumenya madzi. Madzi anagawikananso ndipo Elisa anawoloka powuma – kuonetsa kuti ulamuliro wonse waperekedwa kwa iye tsopano. 'Ana a aneneri' a ku Beteli, amene anali ophunzira enieni othandiza aneneri ovomerezeka, anali mboni za kusintha kwa ulamuliro kuchoka kwa Eliya kupita kwa Elisa. ***(2 Mafumu 2: 13-15)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa ndi Eliya. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro pofunsa ophunzira mafunso awa:<br>a) Kodi ndi malo anayi ati otsiriza amene Eliya anapita asanatengedwe kupita Kumwamba?<br>b) Kodi ***vesi 2, 4 ndi 6*** akufotokoza chiyani za chikhulupiriro cha Elisa?<br>c) Kodi ndi funso liti limene Eliya anafunsa Elisa ndipo yankho lake linali lotani?<br>d) Kodi Eliya anatengedwa motani kupita Kumwamba? | 1) Werengani ***Mateyu 6: 24*** – tikuphunzira kuti Mulungu yekha ndiye akuyenera kukhala Mbuye wathu. Kambiranani kuti izi zinali zoona motani kwa Elisa.<br>2) Werengani ***Aroma 12: 1-2*** – Mulungu akufuna kuti ife tidzipereke monga nsembe zamoyo ndi kusiya moyo wa dziko lapansi. Kambiranani kuti Elisa anachita motani zimenezi. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Moyo wa Eliya unalimbikitsa kwambiri moyo wauzimu wa Elisa. Funsani ophunzira aganizire anthu amene moyo wawo wabwino wauzimu unalimbikitsa moyo wawo wauzimu, mwachitsanzo makolo, aphunzitsi ndi ena ambiri<br>2. Mulungu angathe kugwiritsa ntchito ife kuti tilimbikitse ena pamene timukhulupirira ndi kumutsatira. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Mulungu anayankha pempho la Elisa lofuna magawa awiri chifukwa cholinga chake chinali chabwino, pakuti ankafuna kukwaniritsa zambiri za Mulungu. Akhristu akuyenera kupempha Mulungu kuti achite zinthu zazikulu za Mulungu pa miyoyo yawo.<br>2. Elisa ankakhala pafupi ndi Eliya nthawi zonse, kuzindikira kuti iye ndiye anali m'phunzitsi wake wauzimu. Funsani ana kuti aganizire kuti aphunzitsi awo a moyo wauzimu ndi ndani. |

| | C10 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Elisa<br>Mutu – Elisa athandiza amayi awiri | C10 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Elisa<br>Mutu – Elisa ndi munthu wosauka |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***2 Mafumu 4: 1-37***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aefeso 3: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Utumiki wa Elisa unali wothandiza anthu ena. Mu phunziro lino, iye akuthandiza anthu wosauka ndi achumanso.<br>2. Mulungu akufuna tipereke miyoyo yathu kwa Iye ndi cholinga chakuti mphamvu yake igwire ntchito kudzera mwa ife pamene tikumutumikira. | **Werengani:** ***2 Mafumu 4: 1-44***<br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 4: 33***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anagwiritsa ntchito Elisa mwapadera kwambiri. Elisa ankakhulupirira Mulungu kuti achite zodabwitsa.<br>2. Ife tikuyenera kuonetsa chisamaliro ndi kukhudzidwa kwenikweni ndi anthu ena monga ankachitira Elisa. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira kuti tsopano Elisa watenga udindo wa Eliya. Onse awiri, Eliya ndi Elisa, ankathandiza anthu amene anawazungulira. Pamene Eliya nthawi yake yayitali anakhala akudzudzula za kupembedza mafano ndi zoyipa za nthawi imeneyo, Elisa anakhala nthawi yake yambiri akuonetsa chisamaliro ndi chifundo kwa amene anamuzungulira, monga zimene zili mu phunziroli. | Elisa, mosiyana ndi Eliya amene nthawi yake yambiri ankadzudzula za kupembedza mafano ndi zoyipa, anakhala nthawi zambiri akuonetsa chifundo kwa anthu osowa. Phunziro lino muli zodabwitsa zinayi zimene Mulungu anachita kudzera mwa Elisa: (1) kupereka ndalama kwa mayi wamasiye wosauka; (2) kuukitsa mnyamata wakufa; (3) kuyeretsa chakudya cha kupha; ndi (4) kupereka chakudya kwa anthu 100. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Elisa athandiza mayi wamasiye wosauka amene anali mmodzi mwa akazi a aneneri pomupatsa mafuta ambiri. Izi zinamuthandiza kuti abweze ngongole ndi kuthandiza ana ake awiri aamuna amene anali pa chiopsezo chokhala akapolo ngati akanalephera kubweza ngongole. ***(2 Mafumu 4: 1-7)***<br>2. Elisa anathandizanso mayi wachuma, amene anasamalira Elisa pomupatsa chipinda chogona chapadera. Elisa ankafuna kumubwezera pochita zabwino kwa iye. Iye analibe mwana ndipo Elisa anamuwuza kuti adzabereka mwana wamwamuna. Ngakhale poyamba sanakhulupirire, komabe patapita nthawi anabereka mwanayo. ***(2 Mafumu 4: 8-17)***<br>3. Patapita zaka, mwana uja anadwala ndipo anamwalira. Amayi ake anapita ku Phiri la Karimeli kwa Elisa ndi kukamuwuza kuti iye sanafune kunamizidwa popatsidwa mwana amene wamwalirayo. ***(2 Mafumu 4: 18-28)***<br>4. Ngakhale poyamba Elisa anatuma Gehazi kuti akaukitse mwanayo, Elisa anayenera kupitanso yekha pakuti mwanayo sanauke. Elisa atapumira moyo wake mwa mwanayo, iye anakhala moyo. Mulungu anadalitsa amayi ake kudzera mwa mneneri Elisa, poukitsa mwana wake. ***(2 Mafumu 4: 31-37)***<br>5. Zodabwitsa ziwiri izi zikutikumbutsa kuti palibe chosatheka ndi Mulungu. ***(Onani Luka 1: 37)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa athandziza amayi awiri. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mayi wamasiye anali ndi ngongole ndipo anali ndi mantha chifukwa ana ake akanatengedwa kukhala akapolo. Iye anabwereka mabotolo kwa anzake monga anamulangizira Elisa. Iye anakhuthuliramo mafuta a olivi a m'botolo limodzi lija ndipo mabotolo onse amene anawapeza anadzaza. Atagulitsa mafutawo anabweza ngongole zake. ***(2 Mafumu 4: 1-7)***<br>2. Elisa anathandizanso mayi wachuma, amene anasamalira Elisa pomupatsa chipinda chogona chapadera. Elisa ankafuna kumubwezera pochita zabwino kwa iye. Iye analibe mwana ndipo Elisa anamuwuza kuti adzabereka mwana. ***(2 Mafumu 4: 8-17)***<br>3. Patapita zaka mwana uja anadwala ndipo anamwalira. Amayi ake anapita ku Phiri la Karimeli kwa Elisa ndi kukamuwuza kuti iye sanafune kunamizidwa popatsidwa mwana amene wamwalirayo. ***(2 Mafumu 4: 18-28)***<br>4. Elisa atapumira moyo wake mwa mwanayo, iye anakhala moyo. Mulungu anadalitsa amayi ake kudzera mwa mneneri Elisa, poukitsa mwana wake. ***(2 Mafumu 4: 31-37)***.<br>5. Nthawi imeneyi m'dzikomo munali njala ndipo mmodzi mwa atumiki a Elisa ankaphika chakudya. Pophika chakudyacho anayikamo mpesa za kuthengo. Elisa anathira ufa mu m'phikamo ndipo chakudya chinakhala chabwino ndipo palibe anafa nacho. ***(2 Mafumu 4: 38-41)***<br>6. Pomaliza Elisa anadyetsa anthu 100 malofu buledi ang'onoang'ono makumi awiri. Anakwanira ndipo ena anatsalanso. ***(2 Mafumu 4: 42-44)***<br>7. *Zodabwitsa zinayi izi zikutikumbutsa kuti palibe chosatheka ndi Mulungu.* ***(Onani Luka 1: 37)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa ndi munthu wosauka. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro pofunsa ophunzira mafunso awa:<br>1) Kodi Elisa anagwiritsa ntchito motani mphamvu ya Mulungu imene anapatsidwa?<br>2) Kambiranani ngati Mulungu akuchitabe zodabwitsa lero. | 1) Werengani ***Aefeso 3: 20-21***. Kambiranani ngati pemphero lotamanda Mulungu ndi loyenera pa zodabwitsa zinayi za mu phunziro lino.<br>2) Werengani ***Aefeso 4: 13***. Kambiranani zomwe Mulungu anachita pokwaniritsa zosowa kudzera mwa Elisa kwa anthu amene atchulidwa mu zodabwitsa zinayi m'phunziro lino. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Zodabwitsa izi zikuonetsa kuti ndi kofunika kukoma mtima ndi kusamalira ena. Kodi Akhristu angathandize ena motani?<br>2. Ngati ndinu Mkhristu, kodi mumapempha Mulungu kuti alole mphamvu yake igwire ntchito kudzera mwa inu kuti mumutumikire mokhulupirika? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Mayi wa ku Sunemu anali wokoma mtima kwa Elisa chifukwa anaona kufunika kochita zimenezi. Kodi ife timatha kuzindikira msanga zosowa za anthu ena?<br>2. Ife tikachita zimene Elisa anachita, kupereka kwa ena mosadzikonda, Mulungu nthawi zonse adzatidalitsa. Kodi ophunzira angapereke zitsanzo za kukoma mtima kumene anaonetsa? |

| | **C10 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Elisa**<br>**Mutu – Elisa athandiza msilikali** | **C10 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Elisa**<br>**Mutu – Elisa ndi mkulu wa ankhondo** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***2 Mafumu 5: 1-16***<br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 5: 15***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Utumiki wa zodabwitsa wa Elisa unapitirira ndipo anachiritsa munthu wakhate.<br>2. Khate ndi chifaniziro cha tchimo. Limatilekanitsa ndi Mulungu ndi kutipanga kukhala odetsedwa pamaso pake. Yesu Khristu yekha ndiye yankho la tchimo lathu. | **Werengani:** ***2 Mafumu 5: 1-27***<br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 5: 15***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Utumiki wa zodabwitsa wa Elisa unapitirira ndipo anachiritsa munthu wakhate.<br>2. Khate ndi chifaniziro cha tchimo. Limatilekanitsa ndi Mulungu ndi kutipanga kukhala odetsedwa pamaso pake. Yesu Khristu yekha ndiye yankho la tchimo lathu. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira momwe Mulungu anagwiritsira ntchito Elisa nthawi zambiri zosiyanasiyana. Mu phunziro lino, chodabwitsa cha Elisa – mphamvu yake yakhudza mkulu wa ankhondo wa ku Suria wotchedwa Namani. Iye anali pa ntchito imene ambiri lero akanati inali yabwino kwambiri. Iye anali ndi udindo, mphamvu, khalidwe labwino, ndipo anali wolimba mtima, koma anali wakhate! Khate linaononga zonse! | Mu phunziro lino tipitiriza kuphunzira momwe Mulungu anachitira chodabwitsa kudzera mwa Elisa kuyeretsa Namani, mkulu wa ankhondo a ku Suria, nthenda ya khate. Ife tiphunziranso za mtsikana wa Chiyuda amene anali kapolo ndi wokhulupirika pamaso pa Mulungu koma wosafunikira pamaso pa dziko lapansi. Mulungu anamugwiritsa ntchito kubweretsa machiritso pa Namani. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mkazi wa Namani anali ndi wantchito wamkazi, amene anali kapolo wochokera ku dziko la Israyeli ndipo ankakhulupirira Mulungu. Iye analangiza amayiwa kuti Elisa akanatha kuchiritsa khate la Namani. ***(2 Mafumu 5: 1-3)***<br>2. Namani analakwitsa zinthu zingapo asanatsatire langizo la mtsikanayu. Iye anapita kwa munthu wolakwika, Mfumu Yehoramu – munthu wopembedza mafano, iye anagwiritsa ntchito njira yolakwika pofuna machiritso – golide, siliva ndi zovala, ndipo anapita ndi maganizo olakwika – "Ine ndimaganiza kuti….!" ***(2 Mafumu 5: 4-11)***<br>3. Poyamba Namani anakana malangizo a Elisa oti akasambe mu Mtsinje wa Yordano kasanu ndi kawiri. Koma atachotsa kunyada mwa iye, anakadzinyika m'madzi kasanu ndi kawiri mu Mtsinje wa Yordano. Iye anayeretsedwa ku khate lake. ***(2 Mafumu 5: 12-14)***<br>4. Iye atayeretsedwa, anati, "Ine ndikudziwa." Iye anadziwa kuti kumvera Mawu a Mulungu kudzera mwa Elisa ndiye kunachititsa kuti akhale munthu watsopano! ***(2 Mafumu 5: 15)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa athandiza msilikali. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Asuria anathira nkhondo dziko la Israyeli ndipo anatenga akapolo a Chisrayeli. Mwachitsanzo, Namani anatenga kapolo wachimtsikana. Iye anali wokhulupirira Mulungu woona ndipo analangiza mkazi wa Namani kuti Elisa akanatha kuchiritsa khate la Namani. ***(2 Mafumu 5: 1-3)***<br>2. Mfumu ya Suria inapempha mfumu ya Israyeli, Yehoramu, kuti ichiritse Namani. Mfumu inakwiya kwambiri poganiza kuti kunali kufuna kuti ayambane naye. ***(2 Mafumu 5: 6-7)***<br>3. Elisa anamva za vuto la Namani ndipo anatumiza mawu kwa iye kuti akasambe mu Mtsinje wa Yordano kasanu ndi kawiri ndipo akayeretsedwa. Namani anakwiya kwambiri chifukwa anayankhula naye ngati munthu wamba – iye ankayembekezera ulemu wachifumu! Pamapeto pake antchito ake anakakamiza Namani kuti amvere malangizo a Elisa ndipo anayeretsedwa! Namani anasangalala kwambiri, anathokoza Elisa ndipo analengeza kuti tsopano akudziwa Mulungu woona. ***(2 Mafumu 5: 8-15)***<br>4. Mwachisoni, Gehazi, wantchito wa Elisa anapeza mwayi oti apeze chuma popempha Namani kuti amupatse mphatso zimene Elisa anazikana ndipo ananama za zolinga zake kwa Elisa. Izi zinabweretsa chiweruzo cha Mulungu, ndipo Gehazi anakhala wakhate. ***(2 Mafumu 5: 20-27)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa ndi mkulu wa ankhondo. |
| **KUKUMBUTSANA** | a) Namani anaphunzira kuti sakanatha kusintha moyo wake yekha. Ife tikuyenera kuphunzira kuti ndi Yesu yekha amene angasinthe miyoyo yathu - ***(2 Akorinto 5: 17)***<br>b) Namani anachokera ku dziko limene kunali milungu yambiri; iye anaphunzira kuti kuli Mulungu mmodzi yekha woona. ***(2 Mafumu 5: 15)*** | 1) Werengani ***2 Akorinto 5: 17***. Kambiranani momwe vesi iyi ikufotokozera za kusinthika kwa moyo wa Namani atayeretsedwa, ndi kusintha kumene Mulungu angabweretse m'miyoyo yathu.<br>2) Werengani ***Numeri 32: 23 ndi Agalatiya 6: 7***. Kambiranani zomwe mavesi awiri amenewa akufotokozera zochita za Gehazi. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Pakati pa kupembedza mafano, wantchito uja anakhala mboni ya Mulungu. Akhristu akuyenera kukhala okonzeka kuyankhula ndi kuonetsa chikhulupiriro chawo paliponse pamene angathe kutero.<br>2. Namani anadziwa kuti wayeretsedwa ndipo anasiya kupembedza mafano ndi kutumikira Mulungu woona. Iye anaonetsa moyo wosinthika pa makhalidwe ake. Akhristu akuyenera kuonetsa moyo wawo wam'kati wasintha kudzera m'makhalidwe awo. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ife sitikudziwa zambiri za mtsikana wantchitoyu koma tikudziwa kuti Mulungu anamuyika m'nyumba ya Namani ndi cholinga, ndipo iye anali wokhulupirika. Mulungu anamugwiritsa ntchito pofalitsa Mawu ake kwa anthu ena. Kodi inu mungafalitse Mawu a Mulungu motani kwa ena?<br>2. Kunali kovuta kuti Namani amvere Mawu a Mulungu kuchokera kwa Elisa, koma pamene anamvera moyo wake unasintha kwathunthu. |

| | C10 – KALASI 3<br>Phunziro Lachinayi – Elisa<br>Mutu – Elisa alonjeza chipambano | C10 – KALASI 4<br>Phunziro Lachinayi – Elisa<br>Mutu – Elisa ndi gulu la ankhondo a Suria |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***2 Mafumu 6: 24-25; 7: 1-20***<br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 7: 2***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mfumu ya Aramu inazungulira mzinda wa Samariya. Munalibe chakudya mu mzinda ndipo anthu ankasowa choti achite kuti apeze chakudya.<br>2. Elisa anawuza anthu kuti Mulungu adzawapatsa chipambano chachikulu. | **Werengani:** ***2 Mafumu 6: 24-25; 7: 1-20***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Akorinto 15: 57***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mfumu ya Aramu inazungulira mzinda wa Samariya. Munalibe chakudya mu mzinda ndipo anthu ankasowa choti achite kuti apeze chakudya.<br>2. Elisa anawuza anthu kuti Mulungu adzawapatsa chipambano chachikulu. |
| **MAWU OYAMBA** | Mfumu ya Suria (Aramu) inkafuna kutenga dziko la Israyeli. Gulu lake la ankhondo linazungulira mzinda wa Samariya; chifukwa cha ichi chakudya chinali chosowa komanso chodula kwambiri. Mfumu ya Israyeli inavomereza kuti ndi Mulungu yekha amene akanawathandiza ndi ngati imeneyi. Anthu anayamba kudya anthu anzawo kuti akhute. Iwo ankadzudzula mfumu chifukwa cha kulephera kuchitapo kanthu. Mfumu inkadzudzula Elisa ndipo inapita kuti ikaphe Elisa, koma Elisa anali ndi uthenga wa mfumu wochokera kwa Mulungu. ***(2 Mafumu 6: 32-33 ndi 7: 1-3)*** | Ankhondo a Suria analowa m'dziko la Israyeli ndipo anazungulira Samariya kuti anthu asatulukemo kapena kulowa, zomwe zinabweretsa njala yayikulu. Nthawi zambiri Israyeli ankakana utsogoleri wa Mulungu.<br>Pa ***Deuteronomo 28: 49-57***, analosera za njala ngati imeneyi. Mfumu ya Israyeli inkadzudzula Elisa kuti ndiye anabweretsa njala, pakuti nthawi zambiri aneneri ankanenera za chionongeko chifukwa cha makhalidwe oyipa a mafumu a Israyeli. Mfumu inkadziwanso kuti Elisa anali 'munthu wa Mulungu' ndipo akanatha kuchita chodabwitsa chimene akanafuna koma anakwiya chifukwa palibe chimene Elisa anachita pofuna kupulumutsa Israyeli. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Elisa anawuza mfumu kuti tsiku lotsatiralo adzagulira barele ndi ufa pa mtengo otsika kwambiri komanso anawuza nduna ya mfumu yosakhulupirira kuti sidzadya dalitso la chakudya chimenechi chifukwa sinakhulupirire mawu a Elisa. ***(2 Mafumu 7: 1-3)***<br>2. Anthu anayi amene anali ndi khate anapita ku msasa wa Asuria kuti akapeze chakudya koma iwo anapeza kuti mu msasa munalibe anthu. Mulungu anachitsa Asuria kumva phokoso la gulu lalikulu la nkhondo likubwera, motero anachita mantha ndipo anathawa. ***(2 Mafumu 7: 3-7)***<br>3. Anthu akhate anayi aja anatenga chakudya, ndalama ndi zovala zimene ankhondo a Suria anazisiya ndipo iwo anakawuza mfumu 'nkhani yabwinoyi'. ***(2 Mafumu 7: 8-11)***<br>4. Mfumu inaganiza kuti Asuria abisala, koma inavomera kuti atumize anthu kuti akaone ngati Asuria athawa ndi kusiya katundu wawo yense. ***(2 Mafumu 7: 12-15)***<br>5. Njala inatha ndipo ulosi wa Elisa unakwaniritsidwa. Ufa ndi barele zinali zotsika mtengo tsopano, ndipo nduna ya mfumu yosakhulupirira ija inapondedwa ndi anthu ndi kufa pa chipata cha mzinda. ***(2 Mafumu 7: 16-20)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa alonjeza chipambano. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Elisa analosera za kupulumutsidwa kwa mfumu, koma nduna ya mfumu inati zimenezo sizingachitike. ***(2 Mafumu 7: 1-3)***<br>2. Monga mwa lamulo, akhate sankaloledwa kulowa mu mzinda koma ankadalira thandizo kunja kwa chipata cha mzinda. Koma zinthu zinafika povuta kwambiri, motero iwo anachoka pa chipata cha mzinda ndi kupita ku msasa wa Asuria kuti apeze chakudya ndipo anakapeza kopanda anthu. Yehova anachititsa Asuria kumva phokoso lalikulu la gulu la ankhondo likubwera ndipo iwo anathawa. ***(2 Mafumu 7: 3-7)***<br>3. Poyamba, akhate aja anabisa 'nkhani yabwino' ya zonse zimene anazipeza ndipo anayiwala anzawo amene ankafa ndi njala mu mzinda. Koma kenaka iwo anazindikira kufunika kokafotokoza zomwe apeza kwa mfumu. ***(2 Mafumu 7: 8-11)***<br>4. Mfumu inaganiza kuti Asuria abisala, koma inavomera kuti atumize anthu kuti akayang'ane ku madera onse. Iwo anatsimikiza kuti Asuria anathawa ndipo anthu a Israyeli anatuta zinthu m'matenti a Asuria – njala inatha! ***(2 Mafumu 7:12-16)***<br>5. Ngakhale nduna ya mfumu inaona kutha kwa njala, iyo sinadye nawo chifukwa anthu anayiponda mpaka kufa pa chipata cha mzinda – chifukwa cha kusakhulupirira, monga mmene analonjezera Elisa. ***(2 Mafumu 7: 2 ndi 17-20)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa ndi gulu la ankhondo a Suria. |
| **KUKUMBUTSANA** | Kambiranani ndi ophunzira kuti Mulungu ndiye ankalamulira zochitika pa nthawi yonse ya njala.<br>a) Kugonjetsa zolinga za Satana ndi kuonetsetsa kuti mfumu sinamuphe. (Elisa)<br>b) Kugwiritsa ntchito Elisa pofuna kuonetsa anthu a ku Samariya kuti Mulungu ndi wamphamvuzonse amene angakwaniritse zosowa zawo – chinthu chimene milungu yabodza sikanachita. | 1. Werengani ***Luka 4: 17-19*** – Kambiranani za kuthekera kwa Ambuye Yesu komasula amene ndi akapolo a tchimo.<br>2. Werengani ***Yohane 6: 1-15***. Kambiranani momwe Ambuye Yesu anakwaniritsira zosowa za anthu podyetsa anthu 5,000 ndipo fananizani chodabwitsa cha nthawi ya njala mu phunziro lino. Kambiranani zakuti titha kudalira Mulungu kuti akwaniritse zosowa zathu zonse - ***Mateyu 6: 25-34***. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga anthu akhate aja ankayenera kufotokozera ena 'nkhani yabwino', momwenso amene amatsatira Yesu akuyenera kufotokozera ena 'nkhani yabwino' ya chipulumutso.<br>2. Nthawi zonse Mulungu amakhala akulamulira zochitika – ngakhale mu nyengo zovuta kwambiri m'miyoyo yathu. Ife sitiyenera kukayikira kuthekera kwake kotithandiza kukhala moyo wachipambano ngati ndife ake ndipo timamudalira. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga anthu akhate aja ankayenera kufotokozera ena 'nkhani yabwino', momwenso amene amatsatira Yesu akuyenera kufotokozera ena 'nkhani yabwino' ya chipulumutso. Kodi izi tingachite motani?<br>2. Mulungu amatipatsa chakudya cha tsiku ndi tsiku ndi madalitso ena onse a tsiku lililonse. |

| | **C11 – KALASI 3**<br>**Phunziro Loyamba – Anthu amene Mulungu anawagwiritsa ntchito**<br>**Mutu – Gideoni** | **C11 – KALASI 4**<br>**Phunziro Loyamba – Anthu a Chipangano Chakale**<br>**Mutu – Gideoni** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Oweruza 6: 11-23; 7: 12-22***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Oweruza 6: 16***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pa nthawi yovuta mu mbiri ya Israyeli, Gideoni anasankhidwa kupulumutsa Israyeli m'manja mwa Amidyani.<br>2. Mulungu amagwiritsa ntchito anthu osiyanasiyana kugwira ntchito yake. Ngakhale tili ofowoka ndi olephera, Iye angathe kutigwiritsa ntchito ngati ndife Akhristu. | **Werengani:** ***Oweruza 6: 1-23; 7: 1-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Oweruza 6: 22-23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pa nthawi yovuta mu mbiri ya Israyeli, Gideoni anasankhidwa kupulumutsa Israyeli m'manja mwa Amidyani.<br>2. Ife monga Akhristu tikadalira ndi kumvera Mulungu, Iye adzatipatsa mphamvu zoti timutumikire, ngakhale titadziona kuperewera pa ntchito imene watiyitanira. |
| **MAWU OYAMBA** | Nthawi iyinso Aisrayeli anayiwala Mulungu ndipo ankapembedza milungu yabodza. Mulungu anawalanga polola Amidyani kuwathira nkhondo. Mulungu anatumiza mthenga wapadera kwa Gideoni kudzamuonetsa momwe angagonjetsere Amidyani. Ngakhale Gideoni anadziona kuti sakanatha kugwira ntchito imeneyi, pamapeto pake anamvera Mulungu, ndipo Mulungu anamupatsa chipambano. | Nthawi iyinso Aisrayeli anayiwala Mulungu ndipo ankapembedza milungu yabodza. Mulungu anawalanga polola Amidyani kuwathira nkhondo. Pamene mngelo wa Yehova ankaonekera kwa Gideoni, iye ankapuntha tirigu atabisala m'dzenje kuti Amidyani, amene ankalepheretsa Aisrayeli kukolola, asamuone. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Aisrayeli ankazunzidwa ndi Amidyani ndipo atalirira kwa Mulungu kuti awathandize, poyamba mneneri anatumidwa kudzawakumbutsa za kupembedza mafano kwawo. Kenaka mngelo wa Yehova anaonekera kwa Gideoni ndi kumuwuza kuti Mulungu adzamugwiritsa ntchito kupulumutsa Aisrayeli m'manja mwa Amidyani. ***(6: 7-12)***<br>2. Gideoni anafuna chizindikiro chosonyeza kuti Mulungu adzamugwiritsa ntchito. Iye anakonza chopereka ndipo anabwera nacho kwa mngelo uja amene atachikhudza ndi ndondo yake ndipo chinapserera. Kenaka mngelo uja anazimirira. ***(6: 13-22)***<br>3. Pambuyo pake Gideoni anapita ku msasa wa Amidyani ndipo anamva m'Midyani wina akuwuza mnzake maloto amene anapereka chitsimikizo cha chipambano kwa Gideoni. Iye anabwerera ku msasa wa Aisrayeli kukakonzekera nkhondo. Gideoni anagawa ankhondo ake magulu atatu a anthu 100 gulu lililonse. Iye anapereka lipenga kwa munthu aliyense ndi m'phika wokhala ndi nyali m'kati mwake. Ankhondo a Gideoni atayamba kuyenda kupita ku msasa wa Amidyani, kuwala kwa moto, phokoso la malipenga ndi kusweka kwa miphika zinachititsa mantha Amidyani ndipo anathawa. ***(7: 8-22)***<br>4. Amidyani anagonjetsedwa monga mmene Mulungu ananenera. ***(Oweruza 6: 14)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Gideoni. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Amidyani anali atazunza Israyeli zaka zisanu ndi ziwiri, ndipo izi zinachititsa kuti Aisrayeli abwerere kwa Mulungu. Mneneri anatumizidwa ndi Yehova kuti akafotokozere Aisrayeli kuti ankalangidwa – chifukwa cha kupembedza mafano kwawo. ***(6: 7-10)***<br>2. Mngelo wa Yehova anaonekera kwa Gideoni ndipo analonjeza kumupatsa mphamvu zoti agonjetsere Amidyani. Gideoni anakana chifukwa cha zofowoka zake koma kumapeto anamvera 'chizindikiro' chimene anapempha chitachitika - chakudya chimene anayika pa mwala chinapserera ndi wochokera kwa mngelo wa Yehova. ***(6: 13-23)***<br>3. Mulungu anachepetsa gulu la ankhondo la Aisrayeli kuchokera pa asilikali 32,000 mpaka 300 kuti anthu asakayike kuti chipambano chawo chachokera kwa Mulungu. Iwo ananyamula malipenga, miphika ya dothi ndi nyali, ndipo Gideoni anawalangiza zoyenera kuchita akafika kumene kunali Amidyani. ***(7: 1-8, 16)***<br>4. Phokoso la Aisrayeli lochokera ku malipenga amene ankayimba, phokoso la kusweka kwa miphika ndi kuwala kwa nyali kumene kunaoneka mwadzidzidzi, zinaopseza Amidyani ndipo anachita mantha ndi kuthawa. ***(7: 17-22)***<br>5. *Ngakhale anadabwa ndi ntchito imene Yehova amamupatsa, Gideoni anavomera kugwira ntchitoyo zomwe zinachititsa kuti agonjetse Amidiyani.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Gideoni. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro pofunsa ophunzira mafunso awa:<br>a) Kodi mthenga anali ndani? Kodi uthenga wake unali wotani?<br>b) N'chifukwa chiyani maloto amene anamva Gideoni anali gwero la chilimbikitso kwa iye?<br>c) Kodi Mulungu anapereka njira yotani kwa Gideoni ndi anthu ake kuti agonjetse Amidyani? | 1) Werengani - ***Oweruza 6: 24-40***. Kambiranani monga Gideoni anayikira moyo wake pa chiopsezo pofuna zizindikiro zoti adziwe kuti Mulungu adzamugwiritsa ntchito.<br>2) Werengani - ***1 Akorinto 1: 26-29***. Kambiranani momwe Mulungu amagwiritsira ntchito anthu wamba monga inu ndi ine mu utumiki wake. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ngakhale tonse timakhala ndi nthawi zathu zofowoka monga Gideoni, Mulungu atha kutigwiritsa ntchito.<br>2. Gideoni asanapite ku nkhondo, iye anapembedza Mulungu. ***(Oweruza 7: 15)*** Nthawi zonse ife tikuyenera kumapempha chitsogozo cha Mulungu makamaka mu nyengo zovuta.<br>3. Gideoni ankafuna kukhala chitsanzo monga mtsogoleri. Kodi umu ndi mmene ife timakhalira moyo wathu wa chikhulupiriro cha Chikhristu? ***(Oweruza 7: 17)*** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga Gideoni, ife Akhristu tayitanidwa kuti titumikire Mulungu m'njira yodziwika bwino. Kodi timakhala ndi nthawi yochita zimene Mulungu akufuna kuti tichite kapena timawiringula? Perekani zitsanzo zina.<br>2. Pamene tikufuna chitsogozo cha Mulungu m'miyoyo yathu, kodi timachipeza tikamaphunzira Baibulo? ***(2 Timoteo 3: 16-17)*** Kodi mawu amenewa akutiphunzitsa chiyani za chitsogozo cha Mulungu? |

| | C11 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Anthu amene Mulungu anawagwiritsa ntchito<br>Mutu – Samsoni | C11 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Anthu a Chipangano Chakale<br>Mutu – Samsoni |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Oweruza 16: 6-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Oweruza 16: 28***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Samsoni anabadwa kuti adzathane ndi Afilisti amene analanda dziko lawo.<br>2. Ngakhale Samsoni anali ndi zofowoka zambiri, Mulungu ankamugwiritsa ntchito kugonjetsa Afilisti nthawi zambiri. | **Werengani:** ***Oweruza 13: 1-25; 16: 4-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yakobo 4: 7-8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Samsoni anabadwa kuti adzathane ndi Afilisti amene analanda dziko lawo.<br>2. Ngakhale Samsoni anali ndi zofowoka zambiri, Mulungu ankamugwiritsa ntchito kugonjetsa Afilisti nthawi zambiri. |
| MAWU OYAMBA | Nthawi iyinso Israyeli anakhala pansi pa Afilisti zaka makumi anayi. Samsoni anabadwa m'banja la Manowa ndi mkazi wake ndipo chikonzero cha Mulungu pa moyo wake chinali choti apulumutse Israyeli m'dzanja la Afilisti. Iye anakhala woweruza mu Israyeli zaka makumi awiri. Bwerezani ndi ophunzira zochitika zazikulu mu ***chaputala 13-16***. | Mbiri ya Samsoni ndi nkhani yomvetsa chisoni ya kufowoka kwa munthu, ngakhale kuti iye ndi munthu wamphamvu kwambiri m'Baibulo. Koma ngakhale anali ndi zofowoka, anakwaniritsa cholinga chimene mngelo analengeza pamene anabwera kwa makolo ake iye asanabadwe. ***(Oweruza 13: 5)*** Asanamwalire, Samsoni anavomereza kuti ndi Mulungu yekha amene akamapereka mphamvu. Mulungu anayankha pemphero lake ndipo anaononga kachisi ndi kupha Afilisti amene ankapembedza m'menemo. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Samsoni anakonda mkazi wa Chifilisti wotchedwa Delila. ***(16: 4)***<br>2. Afilisti ankamuopa Samsoni chifukwa cha mphamvu zake zazikulu. Afilisti anamunyengera Delila ndi kumulonjeza ndalama zambiri ngati akanapeza chinsinsi cha mphamvu za Samsoni. Delila anayesera katatu kuti apeze chinsinsicho. Nthawi iliyonse Samsoni ankamunamiza ndipo ankawagonjetsa amene ankabwera kudzamugwira. ***(16: 6-15)***<br>3. Pomaliza Samsoni anafowoka ndipo anawulula chinsinsi cha mphamvu zake. Iye ali mtulo, Afilisti anameta tsitsi lake ndipo mphamvu zake zinachoka koma Samsoni sanazindikire kuti Mulungu wachoka. ***(16: 17-20)***<br>4. Afilisti anamugwira, anakolowola maso ake ndi kumuyika m'ndende. Iwo anakonza chikondwerero chachikulu cha mulungu yawo, Dagoni. Iwo anakakamiza Samsoni kuti awasangalatse. Samsoni anagwira mizati iwiri ya pakati pa kachisiyo, anapemphera kwa Mulungu kuti amupatse mphamvu, anagwetsa mizati ija ndi kupha onse amene anali m'menemo - kuphatikiza iye mwini. ***(16: 21-30)***<br>5. Tikamaganiza za Samsoni, timaganizira kwambiri za mphamvu zake. Koma iye anali ndi zofowoka zambiri chifukwa sanamvere Mulungu ndipo kumapeto kwake anadzibweretsera yekha imfa yowawa.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Samsoni. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mngelo wa Yehova anawuza Manowa ndi mkazi wake kuti iwo adzakhala ndi mwana wamwamuna wotchedwa Samsoni amene adzakhale Mnaziri, munthu wopatulidwa ku ntchito ya Mulungu monga Woweruza mu Israyeli. ***(13: 3-5)***<br>2. Kenaka Samsoni anakhala pa ubwenzi ndi mkazi wa Chifilisti, wotchedwa Delila, amene anamunyengera kuti asokoneza mayitanidwe ake ndi Mulungu. Iye anawulula chinsinsi cha mphamvu zake. Tsitsi lake lalitali sinali chinsinsi cha mphamvu zake koma linkaonetsa kuti iye anali Mnaziri. Unali ubale wake ndi Mulungu umene unamuchititsa kukhala wamphamvu. Atamumeta tsitsi lake, iye analibenso mphamvu. ***(16: 6-20)***<br>3. Afilisti anamugwira, anakolowola maso ake ndi kumuyika m'ndende. Tsopano sankaona ndipo analibe mphamvu. Afilisiti anadzazana mu kachisi wina amene anamangira mulungu wawo wabodza, kuti aseweretse Samsoni. Posatengera kale lake, Samsoni anapemphera kwa Mulungu kuti amupatse mphamvu ndipo nthawi imeneyi Mulungu anayankha pemphero lake. Samsoni anakankha mizati imene inkalimbitsa kachisi ndi kupha onse amene anali m'menemo - kuphatikizapo iye mwini. ***(16: 21-30)***<br>4. *Tikamaganiza za Samsoni, timaganizira kwambiri za mphamvu zake. Koma iye anali ndi zofowoka zambiri chifukwa sanamvere Mulungu ndipo kumapeto kwake anadzibweretsera yekha imfa yowawa.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Samsoni. |
| KUKUMBUTSANA | Bwerezani phunziro pofotokoza za cholinga cha kubadwa kwa Samsoni chomwe mngelo wa Yehova analengeza. ***(Oweruza 13: 5)*** Pamene Samsoni ankamwalira, Mulungu anatembenuza kulephera kwake ndi kukhala chipambano pamene Afilisti ochuluka anafa. ***(Oweruza 16: 30)*** | Werengani ***Oweruza 14: 1-20; 15: 1-20***. Fotokozani kuti machaputala awiri awa sakungoonetsa mphamvu za Samsoni zokha, komanso akuonetsa kufowoka kwa moyo wake. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Nkhani iyi ikuchenjeza Akhristu za kuyesedwa kuti achoke pamaso pa Mulungu ndi zotsatira zake zowawa zimene zimabwera. Koma tikuyenera kukumbukira kuti Mulungu sangatiyiwale ife ndipo nthawi zonse ndi wokonzeka kutikhululukira tikalapa zoyipa zathu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ife tisalole anzathu atikakamiza kuchita zinthu zosakondweretsa Ambuye monga anachitira Samsoni. Ndi udindo wathu kuti tiwakope iwo.<br>2. Chipangano Chatsopano pa ***Ahebri 11: 32-33*** sikuyankhula za kulephera kwa Samsoni, koma zina zabwino zimene iye anachita. Samsoni anabwerera kwa Mulungu asanamwalire ndi kusintha kulephera kwake kukhala chipambano. Izi zikutiphunzitsa ife za kufatsa ndi kusafuna kwa Mulungu kusunga zoyipa zathu. |

| | **C11 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Anthu amene Mulungu anawagwiritsa ntchito**<br>**Mutu – Yona** | **C11 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Anthu a Chipangano Chakale**<br>**Mutu – Yona** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yona 1: 1-7; 3: 1-3***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yona 2: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yona anali mneneri amene sanamvere Mulungu ndi kuphunzira kumvera mu njira yovuta kwambiri.<br>2. Ndi bwino kwambiri kumvera Mulungu m'malo mochita zofuna zathu. | **Werengani:** ***Yona 1: 1-17; 2: 10 - 3: 2***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yona 2: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yona anali mneneri amene sanamvere Mulungu ndi kuphunzira kumvera mu njira yovuta kwambiri.<br>2. Ambuye Yesu akapereka malangizo m'Mawu ake kwa amene amamutsatira, nthawi zonse ndi bwino kuchita zimene Mulungu akutiwuza. |
| **MAWU OYAMBA** | Yona anali wochokera ku Galileya ndipo anawuzidwa kuti apite ku Nineve mu nthawi ya ulamuliro wa Mfumu Yerobiamu, mfumu yamphamvu kwambiri ya Ufumu wa Kumpoto wa Israyeli. Mulungu anatuma Yona kuti akalalikire za kutembenuka mtima kwa anthu a Nineve, mzinda woyipa, likulu la Ufumu wa Ashuri nthawi imeneyo. Aashuri anali anthu oyipa kwambiri. Yona, Myuda, sanafune kupita ndi uthenga wa kutembenuka mtima ndi wa chipulumutso kwa anthu a ku Nineve. Choncho Mulungu anamulanga chifukwa cha kusamvera kwake. | Pa ***2 Mafumu 14: 25***, tikuphunzira kuti Yona anali mwana wa Amitai, mneneri wa ku Galileya. Mulungu anatuma Yona kuti apite kukalalikira ku Nineve nthawi imene Mfumu Yerobiamu Wachiwiri ankalamulira Ufumu wa Kumpoto wa Israyeli. Mzinda wa Nineve unali likulu la Ufumu wa Ashuri ndipo mzinda wa Amitundu komanso wankhanza kwambiri. Yona sanafune kukalalikira za chikondi ndi chifundo cha Mulungu kwa anthu a ku Nineve chifukwa sanali Ayuda ndipo anakula ali ndi chidani pa Ashuri, motero Mulungu anayenera kumulanga chifukwa cha kusamvera kwake. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. **Mayitanidwe a Yona wokalalikira** – Mulungu anatuma Yona kuti akalalikire ku Nineve, koma iye sanamvere ndipo anakwera sitima ya pamadzi kupita ku Tariso, kummwera kwa Sipaniya. Iye anatumidwa kuyenda ulendo wa makilomita 800 koma sanamvere; m'malo mwake anayenda ulendo wa makilomita 3,000 kupita kumadzulo pa sitima ya pamadzi, kuthawa pamaso pa Mulungu ndi pa mphamvu yake. ***(Yona 1: 1-3)***<br>2. **Namondwe pa nyanja** – Panauka namondwe owopsa pa nyanja, sitima pamodzi ndi oyendetsa ake anali pa ngozi yayikulu. Iwo anachita maere kuti adziwe amene ankabweretsa vutoli ndipo anapeza kuti anali Yona. Oyendetsa anachita mantha kwambiri ndipo sanadziwe choyenera kuchita. ***(Yona 1: 4-10)***<br>3. **Yona anaponyedwa m'nyanja ndipo nsomba yayikulu inamumeza** – Oyendetsa sitima mosafuna anamuponya Yona ndipo anakhala m'mimba mwa nsomba masiku atatu usana ndi usiku. ***(Yona 1: 13-17)***<br>4. **Yona apita ku Nineve** – Yona anavomereza kuti chipulumutso ndi cha Yehova, ndipo nsomba inamulavula pa mtunda. Mulungu anamutumanso ku Nineve ndipo Yona anamvera. Iye anachenjeza anthu a ku Nineve za chilango chawo. Zotsatira zake anthu mu mzindawo anatembenuka mtima ndipo anapulumuka kwa chilango chija. ***(Yona 2 ndi 3)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Yona. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. **Mayitanidwe a Yona** – Mulungu anayitana Yona kuti apite ndi kukalalikira ku Nineve chifukwa cha kuyipa kwawo kwakukulu. ***(Yona 1: 1-2)***<br>2. **Kusamvera kwa Yona ndi zotsatira zake** – Yona anayesera kuthawa pamaso pa Mulungu kupita ku Tariso mbali ya kummwera kwa Sipaniya. Yona ali mtulo m'sitima ya pamadzi, kunayamba namondwe wamphamvu amene anayika pa chiopsezo aliyense amene anali m'menemo. Atachita maere zinadziwika kuti anali Yona amene anabweretsa mavuto amenewa. Yona anavomereza tchimo lake ndipo anaponyedwa m'nyanja. Chinsomba chinamumeza ndipo anali m'mimba mwa nsomba masiku atatu usana ndi usiku. ***(Yona 1: 3-17)***<br>3. **Kupulumutsidwa ndi kukonzedwanso** – Yona anapemphera ali m'mimba mwa chinsomba chija ndipo Mulungu anamupulumutsa. Mulungu anamuponyera pa mtunda atavomereza kuti: 'Chipulumutso chimachokera kwa Yehova.' ***(Yona 2: 1-9)***<br>4. **Yona akutumidwanso ku Nineve** – Yona anamvera ndipo anapita ku Nineve kulalalikira uthenga umene Mulungu anamupatsa. Iye atalalikira anthu a mu mzindawo anatembenuka mtima ndipo kupulumuka ku chilango chija. Koma Yona anakwiya poona adani Amitundu a Israyeli akupulumuka! ***(Yona 3 ndi 4)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Yona. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro ili pokambirana ndi ophunzira za momwe Mulungu amakondera dziko lapansi ***(Yohane 3: 16)***. Akumbutseni kuti samakonda Ayuda okha komanso amakonda Amitundu. Yona anali Myuda ndipo anthu a ku Nineve anali Amitundu. Mulungu anaonetsa chikondi chake pokhululukira Yona ndi anthu a ku Nineve pamene analapa. | ***Yona 2: 1-9*** – Kambiranani momwe Yona anapulumukira atapemphera. Pemphero la Yona linali lothokoza komanso la kulapa pamaso pa Mulungu.<br>***Yona 4: 1-11*** – Kambiranani pemphero la Yona ndi chisangalalo chake pamene Mulungu anamupulumutsa komanso za kukwiya kwake pamene Mulungu anapulumutsa anthu a ku Nineve. Mulungu anaphunzitsa Yona kuti chikhululukiro si cha Aisrayeli okha koma ndi cha onse amene amalapa ndi kukhulupirira. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Chipulumutso sichipezeka mwa wina aliyense kupatala mwa Ambuye Yesu okha chifukwa ***'Chipulumutsa chimachokera kwa Yehova.' (Yona 2: 9)*** Ngati tikhulupirira kuti Ambuye Yesu ndiye angatipulumutse, tikuyenera kumumvera powerenga Baibulo ndi kupeza chikonzero chake pa miyoyo yathu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Yona anapatsidwa mwayi wina woti atumikire Mulungu. Mwina tikudzimva kuti ndife osayenera kutumikira Ambuye chifukwa cha zolakwa zathu kapena kusowa luso kwathu. Kodi zolakwa zakale kapena kusowa luso kwathu zimatilepheretsa kutumikira Mulungu? |

| | **C11 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Anthu amene Mulungu anawagwiritsa ntchito**<br>**Mutu – Nehemiya** | **C11 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Anthu a Chipangano Chakale**<br>**Mutu – Nehemiya** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Nehemiya 1: 1-4; 2: 1-8; 4: 6-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Nehemiya 4: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Nehemiya anali munthu wamphamvu wa Mulungu amene Mulungu anagwiritsa ntchito yomanganso makoma a Yerusalemu.<br>2. Mulungu amamva ndi kuyankha pemphero – chinthu choyamba kuti pa zonse ndi kupemphera. | **Werengani:** ***Nehemiya 1: 1-4; 2: 1-8; 4: 6-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Nehemiya 4: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Nehemiya anali munthu wamphamvu wa Mulungu amene Mulungu anagwiritsa ntchito yomanganso makoma a Yerusalemu.<br>2. Mulungu amamva ndi kuyankha pemphero – chinthu choyamba kuti pa zonse ndi kupemphera. Ife timaonetsa Mulungu kuti tikutsimikiza mtima pamene tiphatikiza pemphero pa ntchito yomwe tikukonzekera kugwira. |
| **MAWU OYAMBA** | Nehemiya ankagwira ntchito ku Perisiya yopereka zakumwa kwa Mfumu Aritasasta ndipo unali udindo wofunika kwambiri. Koma iye anasiya ntchito yake yabwino ndi kupita ku Yerusalemu kukathandiza anthu kumanganso makoma a mzinda wa Yerusalemu amene anali atagumulidwa zaka za m'mbuyomo. M'masiku a Nehemiya, makoma a mzindawu anali ofunika kwambiri pa chitetezo chake, kuwuteteza kwa adani a Israyeli. Nehemiya sanali munthu wapemphero kokha, komanso anali mtsogoleri wamphamvu wodziwa zoyenera kuchita komanso wodziwa kulimbikitsa ena kuti amuthandize kuchita zimene akufunazo. | Mulungu anathandiza Nehemiya kuti akwaniritse ntchito imene inkaoneka ngati 'yosatheka'. Nehemiya anali wopereka zakumwa kwa Mfumu Aritasasta, Mfumu ya Perisiya, ndipo mfumu inkamudalira. Iye analinso munthu wa Mulungu, amene ankakhudzidwa ndi Ayuda komanso za kuwonongeka kwa makoma a Yerusalemu. Pamene ankapemphera kwa Mulungu za zimenezi, Mulungu anamutsogolera zoti achite pa ntchito yomanganso makoma a mzinda. Iye anachoka ku Perisiya ndipo anapita ku Yerusalemu. Kuchokera pa chiyambi mpaka kumapeto, iye anapempha thandizo kwa Mulungu ndipo makoma a mzinda anamangidwa mu nthawi yochepa kwambiri, ngakhale ankakumana ndi zotchinga kuchokera kwa adani ake. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. M'bale wa Nehemiya anamufotokozera kuti Ayuda amene anabwerera ku Yerusalemu kuchokera ku ukapolo anali pamavuto aakulu mu mzindamo ndipo makoma ankafunika kumangidwanso. ***(1: 1-3)***<br>2. Nehemiya anakhudzika kwambiri ndi mavuto amenewa ndipo anapemphera ndi kupempha mfumu kuti imulole kuti apite akathandize kumanga makoma a mzindawo. Mfumu inavomera ndipo kwa Nehemiya linali yankho la pemphero lake. ***(2: 1-6)***<br>3. Nehemiya anafika ku Yerusalemu ndipo anayendera makoma. ***(2: 11-16)***<br>4. Atamanga theka la makoma, anayamba kukumana ndi zotsutsa koma Nehemiya anapitirira kupemphera. Iye anayika anthu ena kuti azilondera kuti mwina ena angabwere kudzalimbana nawo. ***(4: 7-9)***<br>5. Nehemiya ndi amene ankagwira nawo ntchito anapitiriza kupemphera, kukhala tcheru ndi kugwira ntchito, motero adani anawo anawasiya. ***(4: 16-19)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Nehemiya. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nehemiya anakhudzika kwambiri ndi mavuto a Yerusalemu. Iye anapemphera kwa Mulungu, ndipo anafunafuna njira yoti akonze zinthu. Iye anasonkhanitsa pamodzi zinthu zake zonse, chidziwitso, luntha ndi utsogoleri ndi kuchita chiganizo cha zomwe ankayenera kuchita. ***(1: 1-10)***<br>2. Mfumu inaona kuti Nehemiya sanali wosangalala. ***(2: 2)*** Chinali chinthu choopsa kwambiri kuoneka wosasangalala pamaso pa mfumu, koma Nehemiya sanachite manyazi kuvomereza mantha ake. M'malo mwake anapemphera ndi kupempha mfumu kuti imulole apite kukathandiza kumanganso makoma a mzinda. Mfumu inavomera, lomwe linali yankho la mapemphero la Nehemiya. ***(2: 1-6)***<br>3. Nehemiya anafika ku Yerusalemu ndipo anayendera makoma. ***(2: 11-16)***<br>4. Atamanga theka la makoma, anayamba kukumana ndi zotsutsa koma Nehemiya anapitirira kupemphera. Iye anayika anthu ena kuti azilondera kuti mwina ena angabwere kudzalimbana nawo. Theka la anthu linkagwira ntchito, pomwe theka lina linkalondera. ***(4: 7-19)***<br>5. Nehemiya analimbikitsa omangawo powatsimikizira kuti 'Mulungu adzatimenyera nkhondo' ndipo kenaka anatsiriza kumanga khoma ndi thandizo la Mulungu pa masiku 52. ***(4: 20 ndi 6: 15)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Nehemiya. |
| **KUKUMBUTSANA** | Werengani ***Akolose 3: 23-24*** ndi kukambirana ndi ophunzira momwe izi zikukhudzira Nehemiya mu phunziro lino. Komanso kambiranani nthawi zimene Nehemiya anapemphera kwa Mulungu ndi kuwuza omanga kuti adalire Mulungu pokhudzana ndi ntchito yomanganso makoma. ***(Chaputala 1: 4; 2: 4; 4: 9; 4: 14 ndi 4: 20)*** | Werengani ***Nehemiya 2: 11-20*** – Kambiranani momwe Nehemiya anachitira poyendera makoma mwezi ukuwala ndi kukhazikitsa njira ya zomwe akuyenera kuchita ndi kufotokozera anthu amene adzamanga makoma. Fotokozani kuti Nehemiya ankadalira Mulungu pa ***vesi 18 ndi 20*** kuti akwaniritse ntchito yomanga makoma a mzinda. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Nehemiya anapemphera kwa Mulungu ndi kubweretsa Mulungu pa ntchito yake ya tsiku ndi tsiku monga mmene tikuyenera kuchitira.<br>2. Nehemiya ndi anthu ake ankapemphera ndi kugwira ntchito, ndiponso ankalondera kuti mwina adani awo atha kubwera. Monga Akhristu, tikuyenera kukhala tcheru ndi Satana amene ndi mdani wa Akhristu ndipo amayesetsa kusokoneza miyoyo yathu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ntchito ya Nehemiya pamaso pa Mulungu inali yoyankhula naye kudzera mu pemphero ndi kuyenda naye pogwiritsa ntchito zimene wawerenga m'Mawu a Mulungu tsiku lililonse. Tikuyenera kupemphera ndi kuwerenga Mabaibulo athu tsiku lililonse ndi kumagwiritsa ntchito zimene tawerengazo.<br>2. Nehemiya anapemphera kwa Mulungu ndi kubweretsa Mulungu pa ntchito yake ya tsiku ndi tsiku monga mmene tikuyenera kuchitira. |

**C12 – KALASI 3**
**Phunziro Loyamba – Nkhani ya Khrisimasi**
**Mutu – Pachiyambi**

**Werengani:** ***Genesis 3: 13-20, Yesaya 7: 14-16***
**Vesi Yoloweza:** ***Yesaya 7: 14***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Nkhani ya Khrisimasi sinayambe mu Betelehemu koma kumayambiriro pa nthawi.
2. Chikonzero cha Mulungu chinali chothetsa tchimo la Adamu ndi Hava potumiza Mwana wake kudzafa.

**C12 – KALASI 4**
**Phunziro Loyamba – Kubadwa kwa Khristu**
**Mutu – Kukwaniritsidwa kwa malonjezo**

**Werengani:** ***Genesis 3: 1-24, Yesaya 7: 14-16***
**Vesi Yoloweza:** ***Yesaya 7: 14***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Ubale wa pakati pa Mulungu ndi munthu unawonongeka pamene Adamu ndi Hava anachimwa m'Munda wa Edene.
2. Mulungu analonjeza kuti kubadwa kwa Ambuye Yesu kudzabwezeretsa ubale wa pakati pa Mulungu ndi munthu, kudzera mu imfa yake ya pa mtanda.

## MAWU OYAMBA

**Kalasi 3:** Adamu ndi Hava asanachimwe m'Munda wa Edene, Mulungu anali kale ndi chikonzero chimene adzachite chifukwa cha kusamvera kwawo. Tchimo la Adamu lili mwa anthu onse. Baibulo lonse likufotokoza nkhani ya chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso, ndipo zomwe zinachititsa kuti Ambuye Yesu abadwe.

**Kalasi 4:** Adamu ndi Hava anaononga ubale wawo ndi Mulungu. Iwo ananamizidwa kuti njira yawo inali yabwino kuposa njira ya Mulungu, motero iwo sanamumvere. Iwo atachita zimenezi, anabisala. Mulungu atayankhula nawo, anayesera kupereka zifukwa zodzitetezera. Tchimo la Adamu lili mwa anthu onse. Baibulo lonse likufotokoza nkhani ya chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso, ndipo zomwe zinachititsa kuti Ambuye Yesu abadwe.

## KUTSIRIZA

**Kalasi 3:**

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Adamu ndi Hava anachimwa m'Munda mwa Edene pamene analephera kumvera zimene Mulungu anawalamula. Mulungu anawafunafuna ndi kuwafunsa kumene anali ndi zomwe anachita. Izi zikuonetsa kuti munthu anali wochimwa, n'chifukwa chake Mulungu anabwera yekha kudzafunafuna munthuyo. ***(Genesis 3: 6-9)***
2. Mulungu analanga njoka (Satana) imene inanamiza Adamu ndi Hava. Anayiwuza kuti idzayesere kufuna kulepheretsa kubwera kwa Mesiya, koma idzagonjetsedwa kudzera mu imfa ndi kuuka kwa akufa kwa Mesiya tsiku lina. ***(Genesis 3: 15)***
3. Mulungu anafotokozera Adamu ndi Hava kuti tchimo lawo lidzakhala ndi zotsatira zake zomwe zidzachititse mkazi kumva ululu pobereka mwana ndipo mwamuna adzatulutsa thukuta pogwira ntchito yopeza chakudya cha banja lake. Mulungu anawawuzanso kuti tsopano adzafa ndi kubwerera ku fumbi chifukwa cha tchimo lawo. ***(Genesis 3: 16-19)***
4. Adamu ndi Hava anathamangitsidwa m'munda, ndipo kenaka Mulungu analonjeza za kubadwa kwa Mpulumutsi kudzera mwa aneneri, makamaka pa ***Yesaya 7: 14***.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Pachiyambi.

**Kalasi 4:**

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Satana ananamiza Hava pomuchititsa kuti akayikire zomwe Mulungu analamula. Hava anachimwa posamvera chenjezo la Mulungu pa ***Genesis 2: 16-17***, ndipo anachititsa kuti Adamu achimwenso. Mulungu atafunsa za tchimo lake, iye anati ndi Hava amene anamuchimwitsa. ***(Genesis 3: 11-12)***
2. Adamu ndi Hava anaphunzira kudzera mu zowawa zimene anakumana nazo kuti Mulungu ndi woyera ndi kuti amadana ndi tchimo ndipo adzalanga ochimwa.
3. Mulungu anawulula chikonzero chake chogonjetsera Satana. Pa ***Genesis 3: 15***, mawu akuti ***'udzaluma chitendene chake'*** akunena za Satana amene adzayesera kugonjetsa Ambuye Yesu Khristu ali pa dziko lapansi. Ndipo mawu akuti, 'Iye adzaphwanya mutu' akuonetsa chipambano cha Ambuye pa mtanda. Kulumidwa chidendene si chinthu choopsa koma kuphwanyidwa mutu. Izi zonse zinali chithunzi cha kugonjetsedwa kwa Satana ndi kuperekedwa kwa chipulumutso pa dziko lonse kudzera mwa Ambuye Yesu Khristu.
4. Kusamvera kwa Adamu ndi Hava ndi kugwa m'Munda wa Edene, zinakhudza chilengedwe chonse. ***(Aroma 5: 12)*** Patapita zaka zambiri, Mulungu kudzera mwa mneneri Yesaya analonjeza za kubadwa kwa Ambuye Yesu kuti adzakhale Mpulumutsi wa dziko lonse. ***(Yesaya 7: 14)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukwaniritsidwa kwa malonjezo.

## KUKUMBUTSANA

**Kalasi 3:** Bwerezani phunziro pokambirana ***Aroma 5: 12*** poyankha mafunso awa:
- Kodi 'munthu mmodzi' mu vesi imeneyi ndi ndani?
- Kodi tchimo ili linachitikira kuti?
- Tchimo linabweretsa imfa ya thupi. Kodi ndi vesi iti pa ***Genesis 3: 13-20***, imene ikutiwuza zimenezi?
- Tchimo linabweretsanso imfa yauzimu ndi kusiyanitsidwa ndi Mulungu. Kodi ndi lonjezo lotani limene Mulungu anapereka kwa njoka losonyeza kuti Ambuye Yesu adzagonjetsa tchimo ndi kutithandiza kuti machimo athu akhululukidwe?

**Kalasi 4:** Gwiritsani ntchito Aroma chaputala 5 kuti muonetse chomwe ife tinali monga ana a Adamu tisanakhulupirire Yesu, komanso chomwe tili lero monga ana a Mulungu, pamene takhulupirira Iye.

| Ana a Adamu: | Ana a Mulungu: |
|---|---|
| Tchimo | Kulungamitsidwa |
| Imfa | Moyo wosatha |
| Kusiyanitsidwa ndi Mulungu | Ubale ndi Mulungu |
| Kusamvera | Kumvera |
| Chiweruzo | Kumasulidwa |
| Lamulo | Chisomo |

## KHALANI MOYO UMENEWU

**Kalasi 3:**

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Monga Adamu ndi Hava anasiyanitsidwa ndi Mulungu chifukwa cha tchimo, ndi zoteronso ndi aliyense lero. Tsindikani kufunika kwa izi.
2. Kodi mungamuyankhe chiyani munthu amene akuti nkhani ya Khrisimasi inayambira mu Betelehemu?
3. Werengani ***Yesaya 7: 14*** ndi ***Mateyu 1: 23***. Ambuye Yesu anabadwa patapita zaka 750 Yesaya atanenera za kubadwa kwake. Yesu anali Mulungu amene anabadwa ngati khanda, motero dzina la Imanueli limatanthauza 'Mulungu ali nafe'.

**Kalasi 4:**

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Pamene Adamu ndi Hava anachimwa, chikumbumtima chawo cha uchimo chinawachititsa kuti abisale pamaso pa Mulungu. Chikumbumtima chathu chimatitsutsa za tchimo lathu. Tingathe kuyesa kubisala koma chimene ife tikuyenera kuchita ndi kupempha Mulungu kuti atikhululukire.
2. Monga Adamu ndi Hava, tonse tinachimwa, koma Ambuye Yesu anafa kuti atichotsere tchimo ndi kutipulumutsa ku zotsatira zake zamuyaya.

| | C12 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Nkhani ya Khrisimasi<br>Mutu – Mthenga wa Mulungu | C12 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Kubadwa kwa Khristu<br>Mutu – Kukumana ndi mavuto |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Mateyu 1: 18-25***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 1: 21***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kubadwa kwa Ambuye Yesu kunali kodabwitsa ndipo kunakwaniritsa maulosi onse a mu Chipangano Chakale.<br>2. Iye ankayenera kutchedwa Yesu, kutanthauza Mpulumutsi. | **Werengani:** ***Mateyu 1: 18-25***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 1: 21***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Lonjezo lakale la kubadwa kwa Ambuye Yesu linali lofunika kuti anthu akhululukidwa machimo awo.<br>2. Tikamadutsa mu nyengo zovuta m'moyo wathu, tikuyenera kukhala ndi chitsimikizo kuti Mulungu adzatithandiza ngati tikumvera Mawu ake ndi kumudalira. |
| **MAWU OYAMBA** | Yambani kufotokoza za phunziro lino pokumbutsa ophunzira kuti maulosi ambiri a mu Chipangano Chakale akulosera za kubwera kwa Ambuye Yesu Khristu. Mu Phunziro 1, tinakumbutsidwa kuti Ambuye Yesu adzayenera kugonjetsa Satana pa mtanda. Yesaya anayankhula za Ambuye Yesu kuti anali 'Mulungu wamphamvu' ***(Yesaya 9: 6)***, kutionetsa kuti Iye anali Mulungu m'thupi la munthu. Mika naye ananenera kuti Yesu adzabadwira ku Betelehemu. ***(Mika 5: 2)***. | Yambani phunziro lino pokumbutsa ophunzira kuti Yesu anabadwa mwa mphamvu ya Mzimu Woyera, ndipo, chifukwa cha ichi, kubadwa kwake timakutchula 'Kubadwa mwa namwali', chomwe ndi chofunika kwambiri pa chikhulupiriro cha Chikhristu. Iye anabadwa woyera, ndipo chifukwa sakanachimwa, anali ndi kuthekera kufa m'malo mwa machimo a munthu ndi kutipanga kukhala ovomerezeka pamaso pa Mulungu. Yesu anabadwa kuchokera mwa mkazi ndipo anali munthu komanso anali Mwana wa Mulungu, wobadwa wopanda tchimo. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kubadwa kwa Ambuye Yesu kunali kosiyana ndi kubadwa kwa wina aliyense – amayi ake anali Mariya, koma abambo ake anali Mulungu. Kuyembekezera kwa Mariya chinali chodabwitsa cha Mzimu Woyera. Yosefe anakwatira Mariya potsatira uthenga wa mngelo. ***(Mateyu 1: 20)***<br>2. Zaka 700 Yesu asanabadwe, Yesaya analosera za kubadwa kwake kodabwitsa ndi kuti adzatchedwa Imanueli, kutanthauza kuti 'Mulungu ali nafe'. ***(Mateyu 1: 22-23)***<br>3. Mwanayo 'adzapulumutsa anthu ku machimo awo' ***(Mateyu 1: 21)*** popita pa mtanda ndi kufera machimo athu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mthenga wa Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yosefe ankayenera kuchita chisankho chovuta pamene anazindikira kuti Mariya anali woyembekezera mwana. Ngakhale Yosefe ankaoneka ngati akuchita chisankho chabwino pofuna kuthetsa chibwenzi chake, upangiri wa Mulungu kudzera kwa mngelo m'maloto unamuthandiza kuchita chiganizo cholondola. ***(Mateyu 1: 19-21)***<br>2. Yesu anabwera pa dziko lapansi kudzatipulumutsa kumphamvu ndi ku zotsatira za tchimo, monga mwa tanthauzo la dzina la Yesu – 'Yehova amapulumutsa'. ***(Mateyu 1: 21)*** Zaka 700 zam'mbuyomo Yesaya ananenera kuti Iye adzabadwa ***(Yesaya 7: 14)*** ndipo adzatchedwa Imanueli, kutanthauza 'Mulungu ali nafe'. Yesu analidi 'ndi ife' pamene anali pa dziko lapansi ndipo ali nafe lero m'miyoyo yathu.<br>3. Yosefe anamvera Mulungu ndipo anapita ndi kupitiriza zokonzekera kukwatira Mariya. Motero iye anakhala abambo a Ambuye Yesu anali pa dziko lapansi pamene Mulungu anali Atate ake a Kumwamba. ***(Mateyu 1: 24-25)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mavuto anakumana nawo. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro lino pofotokoza kuti kubadwa kwa Ambuye Yesu kunalembedwanso mu buku la Luka. Werengani ***Luka 1: 26-35*** ndi kukambirana kufanana kwa pakati ndime iyi ndi ***Mateyu 1: 18-25***. Alembi onse analemba nthawi yomweyo 60AD, koma Mateyu ankalembera Ayuda pamene Luka ankalembera Amitundu. Mulungu ankaonetsetsa kuti uthenga wa kubadwa kwa Yesu ufalikire kulikonse kwa anthu onse pa dziko lapansi, kuphatikiza amene akuchita phunziro lino! | 1. Werengani ***Agalatiya 4: 4 ndi 5***. Kambiranani momwe mavesi amenewa akufotokozera mwachidule za phunziro lino.<br>2. Werengani ***1 Timoteo 1: 15***. Kambiranani momwe akufotokozera mwachidule za kubadwa kwa Khristu.<br>3. Werengani ***1 Yohane 4: 9, 14***. Kambiranani momwe ***vesi 9*** akufotokozera kuti Yesu ndi Mwana yekhayo wa Mulungu. Ndi Yesu yekha amene ali ndi ubale wapadera umenewu ndi Mulungu. ***Vesi 14*** ikunenanso mwachidule zifukwa za kubadwa kwa Khristu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Ntchito ya Yosefe sinali yophweka koma, monga Mariya, iye anadalira Mulungu ndi kusiya zonse m'manja mwake. Ngati timakonda Ambuye Yesu ndipo ndife otsatira ake, ifenso tikuyenera kudalira Mulungu ndi kumvera Mawu ake. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Yosefe anasintha maganizo ake pamene anamva kuchokera kwa mngelo kuti mwana amene ankayembekezera Mariya anali mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. Iye anamvera Mulungu ndi kukwatira Mariya ngakhale kuti mwina ena sanavomerezane nazo. Kodi timapewa kuchita zolondola chifukwa cha zimene ena angaganize kapena timamvera Mulungu?<br>2. Kodi timalola kuti maganizo athu azititsogolera ku zoyipa kapena ku zolondola, kapena timamvera Mawu a Mulungu ndi kulola kuti Iye azitsogolera? |

| | **C12 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Nkhani ya Khrisimasi**<br>**Mutu – Nyenyezi yodabwitsa** | **C12 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Kubadwa kwa Khristu**<br>**Mutu – Kukwaniritsidwa kwa maulosi** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Mateyu 2: 1-12***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 2: 11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Za kubadwa kwa Yesu analosera mneneri Mika ***(Mika 5: 2)*** zaka pafupifupi 700 zisanachitike.<br>2. Mwanayu anali munthu wapadera kwambiri - amene anabadwa kudzakhala Mfumu ya Ayuda - ndipo anzeru a kum'mawa anabwera kudzamupembedza. | **Werengani:** ***Mateyu 2: 1-12***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 2: 6***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Za kubadwa kwa Yesu analosera mneneri Mika ***(Mika 5: 2)*** zaka pafupifupi 700 zisanachitike.<br>2. Anzeru a kum'mawa anayenda mtunda wautali kwambiri kudzaona Yesu. Atamupeza, iwo anali ndi chimwemwe, anamulambira ndi kumupatsa mphatso. |
| **MAWU OYAMBA** | Mu phunziro lino, tikuphunzira kuti anzeru a kummawa anabwera kudzafunafuna 'Mfumu ya Ayuda'. ***(vesi 2)*** Nyenyezi ndiye inawadziwitsa za kubadwa kwa Yesu. Mayendedwe a nyenyezi sanali mmene zimayendera nyenyezi zina chifukwa inawatsogolera anzeruwa ku nyumba imene Yesu ankakhala, ***(vesi 9)*** kenaka inayima! Fotokozani kuti zinthu izi zinali zachilendo ndipo titha kunena kuti chinali chodabwitsa. | Kambiranani za kuti kubadwa kwa Yesu, Mika ndi Yesaya anali atalosera kale. Mika anati Iye adzabadwira ku Betelehemu ndipo adzakhala 'Wolamula mu Israyeli'. Yesaya anagwiritsa ntchito mayina pofotokoza za kubwera kwa Ambuye Yesu: 'Wodabwitsa' kutanthauza woposa ena onse, 'Phungu' kutanthauza wopereka malangizo oyenera, 'Mulungu Wamphamvu' kusonyeza Mulungu wokhala ngati munthu, 'Atate Wosatha' kutanthauza wopanda mathero, ndi 'Kalonga Wamtendere' kutanthauza ulamuliro wake udzakhala wachilungamo ndi wabata. ***(Yesaya 9: 6)*** |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ambuye Yesu atabadwa, Herode, munthu woyipa kwambiri, ndiye anali mfumu. Iye anavutika mu mtima atamva kuti mwana amene wabadwayo adzakhala Mfumu ya Ayuda chifukwa ichi chinali chiopsezo pa udindo wake. ***(2: 3)***<br>2. Herode anayitanitsa atsogoleri achipembedzo a nthawi imeneyo kuti awafunse kumene 'khanda' lomwe ndi Mfumu labadwira, ndipo iwo anawerenga pa ***Mika 5: 2*** pamene akuti ku Betelehemu. Herode anapempha anzeru a kum'mawa kuti adzamuwuze kumene kuli mwanayo akamupeza, kukhala ngati ankafuna kuti akamuone. ***(2: 4-8)***<br>3. Anzeru a kum'mawa anatsogozedwa ndi nyenyezi ku nyumba kumene anapeza mwanayo ali ndi Mariya, amayi ake. Iwo anagwada ndi kulambira Yesu. Iwo anamupatsa mphatso, koma mphatso iliyonse ikutisonyeza chinthu china cha kupambana kwa Mwanayo. Golide akuyankhula za kuti Iye ndi Mulungu, lubani akuyankhula za ungwiro wa moyo wake, ndipo mure akuyankhula za masautso amene adzakumana nawo akadzapachikidwa. ***(2: 9-11)***<br>4. Anzeru a kum'mawa anachenjezedwa m'maloto kuti asapitenso kwa munthu woyipa Herode koma abwerere kwawo kudzera njira ina. Mulungu ndiye ankalamulira! ***(2: 12)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Nyenyezi yodabwitsa. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Anzeru a kum'mawa, amene ayenda mtunda wautali kudzaona khanda limene linabadwa kuti lidzakhale Mfumu, anaona 'nyenyezi yake kum'mawa'. Kaya atha kunena zotani za nyenyezi, kodi Mulungu amene analenga miyamba sakanalenga nyenyezi yapadera kuti idzakhale chizindikiro cha kubadwa kodabwitsa – kufika kwa Mwana wake? ***(2: 1-2)***<br>2. Herode Wotchuka sanali munthu woyenera kulowa ufumu ndipo anavutika mu mtima atamva nkhani ya kubadwa kwa 'Mfumu ya Ayuda'! Herode sankafuna kuti Ayuda akhale pansi pa Mfumu ya Chiyuda, kotero akanachoka mu ulamuliro wa Aroma ndi mwa iye! Ngakhale iye anawuza anzeru a kum'mawa kuti ankafuna kuti akapembedze Yesu, iye ankanama. Cholinga chake chinali chofuna kupha Yesu. ***(2: 3-8)***<br>3. Mwina Ambuye Yesu anali ndi chaka chimodzi kapena ziwiri pamene anzeru a kum'mawa anamupeza. Iwo anali ndi chimwemwe chachikulu ***(Mateyu 2: 10)*** pamene anamupeza ndipo anagwada ndi kumulambira! Iwo anamupatsa mphatso za mtengowapatali zoyenera Mfumu yokha ya m'tsogolo zomwe zinali chizindikiro cha moyo wake. Golide chifukwa Iye anali Mulungu, lubani chifukwa cha moyo wake wangwiro, ndipo mure anali zonunkhiritsa mafuta wodzodza thupi la munthu wakufa. ***(2: 9-11)***<br>4. Anzeru a kum'mawa atachenjezedwa ndi Mulungu anabwerera kwawo kudzera njira ina kupewa kukumana ndi munthu woyipa Herode. ***(2: 12)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukwaniritsidwa kwa maulosi. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro ili pofunsa mafunso kuti mutsimikize ngati ophunzira amva zomwe aphunzira. Mafunso akhale ofanana ndi zomwe zili mu Phunziro 3 kuti ophunzira athe kuyankha molondola. | Bwerezani Phunziro. Fotokozani kuti ***Yesaya 9: 6*** ndi ***Mika 5: 2*** zakwaniritsidwa kale mu phunziro lino koma ***Yohane 14: 1-6*** sanakwaniritsidwe. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Anzeru a kum'mawa anafunafuna Yesu ndipo anamupeza. Nthawi zambiri amanena kuti "Anthu anzeru akufunafunabe Yesu."<br>2. Anzeru a kum'mawa atalowa m'nyumba anapembedza Yesu, osati Mariya kapena Yosefe. Ndi Yesu yekha, Mwana wa Mulungu, amene akuyenera kutamandidwa ndi kupembedzedwa. Kambiranani kuti izi zikutanthauza chiyani kwa ophunzira. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Anzeru a kum'mawa anapereka mphatso zawo zabwino kwambiri. Kodi Akhristu angaphunzire chiyani kuchokera pa kudzipereka kotere?<br>2. Anzeru a kum'mawa atamupeza Yesu, anachenjezedwa kuti abwerere kwawo podzera njira ina. Moyo wa Mkhristu nthawi zonse sumakhala osalala. Kodi Akhristu angachite chiyani kuti azidziwa kuti ali pansi pa chitetezo cha Mulungu? |

| | C12 – KALASI 3<br>Phunziro Lachinayi – Nkhani ya Khrisimasi<br>Mutu – Kuthawa usiku! | C12 – KALASI 4<br>Phunziro Lachinayi – Kubadwa kwa Khristu<br>Mutu – Kuyamba kwa masautso |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Mateyu 2: 13-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Yohane 3: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kubadwa kwa Ambuye Yesu ndi chitetezo chake zinakonzedwa mosamalitsa ndi Mulungu monga mmene analosera aneneri zaka zambiri m'mbuyomo.<br>2. Satana sanathe kuononga Ambuye Yesu chifukwa Mulungu analonjeza m'Munda wa Edene kuti Ambuye Yesu adzagonjetsa Satana pamene Iye adzafe pa mtanda. | **Werengani:** ***Mateyu 2: 13-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 2: 14***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Herode anali mfumu amene anasankhidwa ndi Aroma koma Yesu anali Mfumu enieni, motero palibe amene akanatchinga malo amene Mulungu anamupatsa Mwana wake.<br>2. Ambuye Yesu anakhala munthu kuti adzafe ndi kuuka ndi cholinga chofuna kuononga mphamvu za mdierekezi pa imfa monga ananenera pa ***Genesis 3: 15***. |
| **MAWU OYAMBA** | Zokambirana zikhazikike pa anthu amene lero pa dziko lapansi akuzunzidwa ku mayiko monga Suria, kumene anthu ena anathawa ndi kukakhala ku mayiko ena monga anthu othawa kwawo. Kuyambira ali khanda, chiopsezo chofuna kuphedwa chinali pa Ambuye Yesu ngakhale anabwera kudzafera ochimwa, koma inkayenera kukhala nthawi yoyikika ndi Mulungu. Yosefe anachenjezedwa ndi mngelo wa Ambuye kuti athawire ku Aigupto ndi banja lake – iye anakakhala ngati munthu wothawa kwawo pofuna kuthawa mkwiyo wa Herode. Ife sitidziwa kuti anakhala nthawi yayitali motani ku Aigupto. | Yambani phunziro pofunsa ngati alipo amene anamva za Sphinx ndi Great Pyramids a ku Aigupto. Fotokozani kuti zimenezi zinali gawo limodzi la chikhalidwe cha Aaigupto mu nthawi ya Yesu monga mmene zilili leronso. Komanso nthawi imeneyo kunali madera ena a Ayuda m'mizinda yayikulu mu Aigupto amene anali pansi pa Aroma monganso anthu a ku Yudeya ndi ku Galileya. Izi zinathandiza Yosefe, Mariya ndi Yesu kukhala ku Aigupto kwa kanthawi. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kwa nthawi yachinayi, pa ***Mateyu 2***, tikukumbutsidwa za kukwaniritsidwa kwa ulosi wina wa Hoseya ***(Hoseya 11: 1)*** amene ananena kuti Yesu adzayitanidwa kuchokera ku Aigupto. Ulosi uwu unakwaniritsidwa pamene Yosefe ndi banja lake anabwerera ku Israyeli kuchokera ku Aigupto. ***(2: 15)***<br>2. Pamene Herode anazindikira kuti chiwembu chofuna kupeza mwana Yesu chalephereka, analamula kuti ana onse aamuna a zaka ziwiri mu Betelehemu ndi madera ozungulira aphedwe. Izi zinabweretsa chisoni chachikulu kwa makolo amene ana awo anaphedwa pamene 'Wolowam'malo' anali ku Aigupto. ***(2: 16-18)*** Chinali chikonzero cha mdierekezi kuti aononge Yesu, koma analephera.<br>3. Mngelo wa Ambuye anawuza Yosefe pamene zinthu zinali bwino kuti abwerere ku dziko la Israyeli Herode atamwalira. Koma Yosefe atadziwa kuti mwana wa Herode ndiye analowa ufumu, anaganiza kuti asapite ku Yudeya koma apite kumpoto ku Galileya ndi kukhala ku Nazarete. Mulungu ndiye ankatsogolera mayendedwe a mwanayo monga mmene ananenera aneneri! ***(2: 19-23)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kuthawa usiku! | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Maloto ake oyamba kapena masomphenya amene Yosefe analandira ku Mulungu anawuzidwa kuti mwana wa Mariya adzatchedwa Yesu. ***(Mateyu 1: 20-21)*** M'maloto achiwiri kapena masomphenya anawuzidwa monga angatetezere moyo wa mwanayo pothawira ku Aigupto. Yosefe anamveranso Mawu a Mulungu. ***(Mateyu 2: 13-15)***<br>2. Herode ankachita mantha ndi Mfumu yatsopano yomwe yabadwa kuti tsiku lina idzatenga mpando wake waufumu, choncho iye anapha ana onse aamuna a zaka ziwiri kapena kucheperapo mu Betelehemu ndi ku madera ozungulira. Koma Mulungu ankalamulira zonse ndipo sanalole kuti Herode aphe Yesu. Herode sanamvetse bwino za chimene Ambuye Yesu anabwera kudzachita – Iye sankafuna mpando wa Herode; Iye ankafuna kukhala Mfumu ya moyo wa Herode. ***(Mateyu 2: 16-18)***<br>3. Herode atamwalira mu 4BC, mwana wake Arikelao, mtsogoleri woyipa kwambiri, ndiye ankalamulira zigawo za Yudeya ndi Samariya komwe kunali Yerusalemu ndi Betelehemu. Mulungu sanafune Yosefe kuti apite ku madera amenewa, ngakhale Yosefe sanafunenso. Mulungu anamutsogolera kupita ku kumpoto ku Nazarete ku Galileya. ***(Mateyu 2: 21-23)***<br>4. Yesu anakulira m'mudzi wonyozeka wa Nazareti zomwe zikutanthauza kuti ngakhalenso Iye ankanyozedwa monga ena onse a ku Nazarete.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kuyambika kwa masautso. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziro pofunsa mafunso awa:<br>a) N'chifukwa chiyani Yosefe, Mariya ndi Yesu anathawira ku Aigupto?<br>b) N'chifukwa chiyani Herode anapha ana aamuna a mu Betelehemu?<br>c) N'chifukwa chiyani banja ili linakakhala ku Nazarete?<br>d) N'chifukwa chiyani nkhani ya Khrisimasi ndi ya chisoni komanso ya chimwemwe? | 1) Werengani ***Genesis 3: 15*** – Onetsetsani kuti ophunzira amvetsetsa kuti vesi imeneyi ikunena za m'tsogolo nthawi imene Ambuye Yesu adzafe ndi kumulanda Satana mphamvu zake.<br>2) Werengani ***Machitidwe 10: 38-43*** – Kambiranani momwe ulaliki wamphamvu wa Petro ukufotokozera zonse za phunziroli mwachidule. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Pa ***Luka 2: 11***, pamene mngelo analengeza za kubadwa kwa Yesu, iye anati Yesu ndi 'Mpulumutsi' ndi 'Ambuye'. Akhristu amakhulupirira kuti ndi Mpulumutsi ndi Ambuye awoawo.<br>2. Kambiranani ndi ophunzira momwe maphunziro ano awathandizira kumvetsetsa za kufunika kwa Chipangano Chakale. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga Yosefe, ife tikuyenera kufuna chitsogozo cha Mulungu pa miyoyo yathu.<br>2. Yesu atabadwa, Herode anabweretsa masautso aakulu. Koma Mulungu ndiye ankalamulira ndi kuteteza mfumu yomwe yabadwa. Kodi izi zingalimbikitse motani Mkhristu amene akukumana masautso lero? |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Lachitatu**
- Ophunzira sangatsirize maphunziro awa popanda kuwerenga Baibulo ndipo akuyenera kuwerenga ndime imodzi kapena zambiri.
- Kafunsidwe n'kosiyanasiyana, pena pali mabokosi, pena pali mawu amene akusowa ndi njira zina zambiri.
- Mafunso akonzedwa kuti aziyankhidwa kuchokera m'baibulo la Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero ndi Buku Lopatulika ndi Mawu a Mulungu.
- Cholinga chathu n'chakuti ophunzira onse, kaya akugwiritsa Baibulo la mtundu wanji, azitha kuyankha mafunso.
- Sabata lililonse lili ndi marikisi 20 ndipo pa mwezi pali marikisi 80, ngati munthu wakhonza bwino maphunziro onse.
- Kalasi Lachitatu - Pali marikisi imodzi pa yankho, monga momwe tasonyezera.

**Maphunziro a Kalasi Lachinayi**
- Awa ndi maphunziro ovutirapo kusiyana ndi Maphunziro a Kalasi Lachitatu.
- Muli mafunso ovutirapo ofuna mayankho.
- Marikisi 20 pa sabata ndi marikisi makumi 80 pa mwezi ngati amaliza maphunziro molondola ndiponso mafunso onse ali ndi mayankho ake.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**
Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.
Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**KALASI Lachitatu**
**Ndemanga zina**
"Ntchito yabwino kwambiri! Inu munamvetsa bwino mafunso onse. Ine ndasangalala ndi yankho la funso lotsiriza limene mwaliyankha bwino kwambiri."
"Moni, Yonatani. Ndikuyamika chifukwa cha kulimbikira kwako. Ndi zosangalatsa kwambiri kuti wayesetsa kuyankha mafunso onse. Ine ndalemba mayankho a mafunso ena amene sunayankhe."

**Ndemanga zauzimu**
"Mose anali ndi mavuto ndi ana a Israyeli, koma Mulungu sanamusiye yekha kuti athetse mavutowo."
"Yosefe sanayiwale kuti abambo ake anamuphunzitsa kukonda Mulungu. Iye anakumbukira zimenezi ngakhale anali kutali ndi kwawo."
"Bartimeyu anatsimikiza mtima zofuna kulandira kuchokera kwa Ambuye Yesu. Iye sanakhumudwitsidwe chifukwa tsopano ankatha kuona ndipo anadziwa kuti Ambuye Yesu anali munthu wapadera kwambiri."

**KALASI Lachinayi**
**Ndemanga zina**
"Maphunziro enanso abwino kwambiri. Zikuoneka kuti tsopano ukumvetsa bwino Nkhani za m'Baibulo ndipo ndikukhulupirira kuti wasangalala nazo. Zikomo kwambiri chifukwa chokhala ndi nthawi yokwanira yochita mosamala maphunzirowa. Zikanatheka kuchita mofulumira, choncho ine ndi kuyamika kwambiri."
"Rakele, wayetsetsa ndithu. Ine ndikaona mayankho akowa, zikuonetsa kuti sunamvetse bwino Nkhani za m'Baibulo. Bwanji uwerengenso zimenezi."

**Ndemanga zauzimu**
"Mafanizo nthawi zina amatchedwa nkhani wamba koma zokhala ndi matanthauzo akumwamba kapena ozama. Kodi ungaganizire tanthauzo lozama la fanizo lomwe lili mu Phunziro 3?"
"Stefano anafa imfa yowawa kwambiri, koma iye sanachite mantha ndi imfa, chifukwa ankadziwa kuti anali ndi Mulungu, ndipo ankadziwa kuti akakhala ndi Ambuye Yesu Kumwamba."

| Zoonjezera A – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| C7 | Davide | **Kusankha mfumu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-david-anointed/ |
| | | **Kumenyana ndi Goliati** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-goliath/ |
| | | **Kukhala ndi Sauli** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-jonathan/ |
| | | **Pa ubwenzi ndi Jonatani** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-jonathan/ |
| | | |
| C8 | Yoswa | **Kutsogolera anthu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-joshua/ |
| | | **Kuzonda dziko** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-rahab-spies/ |
| | | **Kuwoloka mtsinje** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-jordan/ |
| | | **Kumvera Yehova** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-jericho/ |

| Zoonjezera A – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| C7 | Davide | **Kusankha Mfumu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-david-anointed/ |
| | | **Kugonjetsa munthu wamphamvu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-goliath/ |
| | | **Kupirira m'mavuto** |
| | | /https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-jonathan/ |
| | | **Kusamalira ena** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-mephibosheth/ |
| | | |
| C8 | Yoswa | **Mtsogoleri watsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-joshua/ |
| | | **Kutumiza azondi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-rahab-spies/ |
| | | **Kuwoloka Yordano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-jordan/ |
| | | **Kugonjetsa ndi Kugonjetsedwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-jericho/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-achan/ |

| Zoonjezera B – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| C9 | Eliya | **Kulamulidwa ndi Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-brook/ |
| | | **Kusamalidwa ndi Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-widow-boy/ |
| | | **Kutsutsana ndi aneneri a Baala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-carmel/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-prays-rain/ |
| | | **Kosokonekera chifukwa cha mantha** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-elisha/ |
| | | |
| C10 | Elisa | **Eliya akumana ndi Elisa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-elisha/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-chariot/ |
| | | **Elisa athandiza amayi awiri** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-boy/ |
| | | **Elisa athandiza msilikali** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-naaman/ |
| | | **Elisa alonjeza chipambano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-siege/ |

| Zoonjezera B – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| C9 | Eliya | **Chilango cha Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-029-lame-man/ |
| | | **Chisamaliro cha Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-widow-boy/ |
| | | **Mphamvu ya Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-carmel/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-prays-rain/ |
| | | **Kupezeka kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/elijah-horeb/ |
| | | |
| C10 | Elisa | **Elisa ndi Eliya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-chariot/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-elisha/ |
| | | **Elisa ndi munthu wosauka** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-boy/ |
| | | **Elisa ndi mkulu wa ankhondo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-naaman/ |
| | | **Elisa ndi gulu la ankhondo a Suria** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-siege/ |

| Zoonjezera C – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C11** | **Anthu amene Mulungu** | **Gideoni** |
| | **anawagwiritsa ntchito** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gideon-fleece/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gideon-midianites/ |
| | | **Samsoni** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samson-hair/ |
| | | **Yona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jonah-disobeys/ |
| | | **Nehemiya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/nehemiah-1/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/nehemiah-2/ |
| | | |
| **C12** | **Nkhani ya Khrisimasi** | **Pachiyambi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/ |
| | | **Mthenga wa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/ |
| | | **Nyenyezi yodabwitsa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-wisemen/ |
| | | **Kuthawa usiku!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-wisemen/ |

| Zoonjezera C – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C11** | **Anthu amene Mulungu** | **Gideoni** |
| | **anawagwiritsa ntchito** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gideon-fleece/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gideon-midianites/ |
| | | **Samsoni** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samson-riddle/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samson-hair/ |
| | | **Yona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jonah-disobeys/ |
| | | **Nehemiya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/nehemiah-1/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/nehemiah-2/ |
| | | |
| **C12** | **Kubadwa kwa Khristu** | **Kukwaniritsidwa kwa malonjezo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/ |
| | | **Kukumana ndi mavuto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/ |
| | | **Kukwaniritsidwa kwa maulosi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-wisemen/ |
| | | **Kuyamba kwa masautso** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-wisemen/ |

© Bible Educational Services 2023

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 08/2025
(Chichewa)